# *Mulungu Wa M'badwo Woipa Uno*

[M'bale Orman Neville akuti, "Lipoti ili, utachitika msonkhano walimodzi wa gulu la madikoni ndi matrastii a pa kachisi Lachisanu usiku, ife tikuwerenga zogwirizana izi zomwe ndi za mwamuna aliyense, mkazi aliyense, yemwe ali wotsatira wokhazikika wa utumiki uwu, yemwe ayenera kudziwa malingaliro a bodi, m'busa ndi wothandizira m'busa. Ine ndiwerenga zogwirizana izi mmawa uno. Aliyense apereke chidwi chenicheni ndi tcheru kwa izo momwe inu mungathere." M'bale Neville akuwerenga zogwirizana zotsatirazi.]

["Zogwirizana izi zinapangidwa ndipo zinavomerezedwa ndi bodi la matrasti, ndi madikoni mu mgwirizano wathunthu ndi m'busa ndi womthandizira m'busa.]

["Matepi onse a maulaliki a M'busa William Branham ndi oti azipangidwa ndi Fred Sothmann yekha, kufikira zitadzadziwitsidwa mtsogolo ndi bodi. Ife pa nthawi ino sitikuuzindikira utumiki waulere uliwonse wa matepi. Matepi awa ali ndi umwini, ndipo sangachulukitsidwe ndi munthu wina aliyense kuposa Fred Sothmann popanda chilolezo cholembedwa ndi iyeyo.]

["Nambala thuu. Pasakhale munthu wochititsa misonkhano, kugulitsa mabuku kapena matepi, kulemba matraki, kugawa nsalu za pemphero kapena makhadi a mtundu uliwonse, kapena kupemphetsa mphatso zirizonse, wosazindikiridwa ndi mpingo uno kapena m'busa wake. Iwo azichita izi mwachinyengo, ndipo sanapatsidwe ulamuliro kuti azichita zimenezo.]

["Firii. Mpingo uno sumatumiza azitumiki kunja kupatula m'busa wake, M'busa William Branham, kuti azikachititsa misonkhano kulikonseko.]

["Zifukwa za zogwirizana izi ndi zakuti:]

["Zanenedwa kwa ife kuti atumiki akuwoloka dzikoli ndi kumakalowa mu ziyanjano zina, kumakanena kuti iwowo ali pachiyanjano, ndiponso atumidwa ndi mpingo uno kuti azikachititsa misonkhano imeneyi.]

["Zanenedwanso kwa ife kuti anthu akumadinda makhadi ndi matraki, akutumiza nsalu za mapemphero ndi zina zotero, ngati kuti alolezedwa kuti achite zimenezo ndi mpingo uno ndi m'busa wake, zimene si zoona. Zidzayamikiridwa ngati inu mutawudziwitsa mpingo za munthu aliyense wopezeka akuchita zimenezi.]

[“Zogwirizana izi zawerengedwa ndipo zavomerezedwa ndi m’busa Rev. William Branham, wothandizira m’busa Rev. Orman Neville, ndi gulu la matrastii ndi madikoni.”—Mkonzi.]

[M’bale Neville kenako akuti, “Ambuye akudalitseni inu.” Mu msonkhano wa usiku, 65-0801E, M’bale Branham akunena momwe gulu la mpingo linapangira zigamulo izi. Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

Zinthu zonse nzotheka, kungokhulupira;
Kungokhulupira, kungokhulupira,
Zonse nzotheka, khulu . . .

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

Wokondedwa Atate akumwamba, ife tiri oyamikira mmawa uno kuti ife tikhoza kukhulupirira. Izo zatheka ndi Magazi okhetsedwa a Mwana Wanu, Yesu, kuti ife tikhale otenga nawo a chisomo Chake; ndi kudzakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, kudzera mu kumvera ku imfa Kwake pa mtanda, kulungamitsidwa pa kukhulupirira pa Iye ndi chiukitsiro Chake, ndipo tsopano Mzimu Woyera waikidwa mmitima mwathu.

2 Ife tiri oyamikira chifukwa cha mwayi uwu kuti tabwera pano mmawa uno kuti tidzagawane malingaliro athu ndi mapembedzero athu, kufotokozera mwa nyimbo, maumboni, kuwerenga kwa Masalmo, kuwerenga kwa Mawu Anu, ndi kudikirira mwaulemu pa Mzimu Woyera kuti upereke kwa ife Uthenga woikidwira ora lino. Perekani izi, Ambuye. Mulole ife tikapindule pakukhala pano lero. Ndipo pamene ife tizichoka mnyumbayi, mulole ife tikanene monga iwo amene ankachokera ku Emau, “Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu pamene Iye amalankhula nafe mmawa uja?” Perekani zinthu izi, Mulungu Wamuyaya, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Mukhoza kukhala.

3 Mmawa wabwino, abwenzi, pano, kuno pa kachisi ndi kwa abwenzi athu kudutsa fukoli, njira yonse kuchokera ku Gombe la Kumadzulo, ukonso mmawa uno, mpaka ku Gombe la Kummawa, ndi kumpoto ndi kummwera, pa kulumikiza kwa lamya.

4 Ndi tsiku labwino kuno mu Indiana, pang’ono, la mitambo pang’ono, lozizira, labwino kwambiri. Kachisi wadzadza, mpaka panja uko ndi kuzungulira makoma. Ife tiri pansi pa kuyembekezera kwakukulu kuti Ambuye atichezera ife lero. Ndipo ife tikuyembekeza kuti Mulungu wakupatsani inu tsiku labwino kulikonse kumene inu muli. Ndipo ilo ndi tsiku labwino, pakuti Ambuye walipereka ilo. Ziribe kanthu kuti nyengo ili bwanji, ilo ndi tsiku labwino. Ndife okondwa kuti tiri muno, wokondwa panobe kuti ife tiri nawo mwayi kuti tikafotokoze kwa dziko chikhulupiriro chathu mwa Yesu Khristu. Ndipo ife tikufuna kuti titenge mwayi uliwonse umene ife tingathe kuti

tipereke kufotokozera kwathu kwa chikondi Chake ndi chimene Iye watichitira ife. Lero ife tiri . . .

5 Ine ndinapatsidwa, mphindi pang'ono zapitazo, cho—choti ndilengeze, ndiyeno ine ndiri ndi zinthu pang'ono apa zimene ine ndikukhumba kuti ndizinene. Ndipo chimodzi cha izo, cholengeza chimene ndinapatsidwa ine cha msonkhano wa bodi usiku wina. Ndipo pali dikoni mmodzi wochokera pa mpingo yemwe wapeza nyumba ku Arizona, yemwe ali M'bale Collins, m'bale wathu wochirimika. Ndipo pamene iye wachokapo, iwo, bodi, yasankha M'bale Charlie Cox kuti atenge malo ake pamene iye akhala atapita. Ndipo M'bale Charlie Cox wasankhidwa movomerezedwa ndi matrasti . . . kapena bodi ya madikoni ya mpingo uno, kuti atenge ofesi ya M'bale Collins, pamene iye kulibeko.

6 Ndipo chinthu chimene ine ndikufuna kuti ndinene, panonso, ine ndikufuna kuti ndikuthokozeni anthu nonse inu, chifukwa ena a inu mukhoza kukhala mutapita kwanu tisanayambe msonkhano wa machiritso usikuuno, chifukwa cha mphatso zabwino zazing'ono, zochitira umboni. Zakudya zambiri zabweretsedwa kwa ife kuyambira pamene ife tinabwera kuno. Ndipo kuchokera kwa akazi anga ndi ine, ndi banja langa, ife ndithudi tikuyamikira izo. Nthawizina ine ndimaiwala ngakhale kuti ndinene chirichonse cha izo. Ndimakhala wotanganidwa kwambiri, inu mukudziwa. Malingaliro anga amakhala mu kamvulumvulu woteroyo nthawi zonse. Inu mukhoza kulingalira chimene izo ziri, za anthu, osati kokha ochokera pano pa tchalitchi chino, koma kuchokera pa dziko lonse. Mukuona? Ndipo izo zimakhala ngati zimakuika iwe mu kamvulumvulu nthawizonse.

7 Winawake amanena za kudalitsa kwa ana, ndi mautumiki a ubatizo, ndi zina zotero. Zimenezo ndi zabwino kwambiri. Ndikukhumba ine ndikanachita izo, koma izo basi ndi zopindika kwambiri, ine—ine ndiribe nthawi. Ine ndiyenera kuti ndiyike malingaliro anga pa izi, Uthenga uwu. Inu mukudziwa Baibulo linanena kwa atumwi, kapena . . . Atumwi, kani, mu Baibulo, anati, "Pitani, mukadziyang'anire nokha, pakati panu, amuna a mbiri yabwino, ndi owonamtima ndi odzazidwa ndi Mzimu Woyera, kuti iwo azisamalira zochitika." Ndipo ine ndinamuuza Billy . . .

Iye anati, "Kodi inu mudalitsa ana nthawi ino, adadi?"

Ine ndinati, "O, mai!" Mukuona? Ngati . . . Ife tiri nawo ambiri a iwo amene akudikirira kuti adalitsidwe, ndipo izo nzoona, ine ndikungosowa kuti ndidzabwererenso ndi kudzatenga tsiku la padera la kudalitsa ana. Kotero ine ndikufuna kuti ndichite zimenezo, tsopano.

8 Koma ife tikufuna kuthokoza mmodzi aliyense wa inu kuchokera mmitima mwathu; mkazanga, ine, ndi banja lathu.

Anthu mwatibweretsera ife chakudya cha nzitini, nyemba zaziwisi, mavembe, akaimbi, o, nthuza. Basi chirichonse chimene chingaganiziridwe, iwo atibweretsera izo.

9 M'bale wofunika ndi mlongo wake, tsiku lina, anatibweretsera ife nkhukutembo yaikulu. Ine ndikudyabe iyo. Ndipo kotero basi . . . O, ndipo ine ndiyenera ndiitsirizitse iyo ine ndisananyamuke, ine ndikuganiza. Kotero ngati ine sinditero, iye adzaitenga iyo tikamadzapita. Ndipo kotero—kotero ife tidza . . . Ife ndithudi tiri oyamikira zinthu izi. Ine ndikuwadziwa anthu ambiri; ena a iwo ine sindikuwadziwa. Iwo amakhala akudikirira pakhonde pamene ife tikulowa. Ndipo kotero ine ndithudi ndikuyamikira izo.

Ndipo ambiri ine ndikuwadziwa. Ine ndiri . . . Ine ndawawona ambiri, ndipo alipo ambiri amene ine sindikwanitsa kuti ndiwawone. Ine—ine ndikutsimikiza kuti aliyense akumvetsa kuti ine—ine ndimafuna kufikira kwa aliyense ngati ine ndingathe, koma ine ndiri ndekha. Mukuona? Kwa . . . Ine sindingathe kufikira kwa aliyense. Ine ndikuchita chirichonse chimene ine ndikudziwa kuchichita kwake.

10 Kotero, Mulungu akhale nanu. Ine ndikutsimikiza kuti alipo Mmodzi yemwe ati azikhala ndi inu; ameneyo ndi Yesu Khristu, ndipo Iye akhoza kukhala. Iyeyo ali Munthu yekhayo yemwe ali wopezeka ponseponse. Ndipo Iye alinso wamphamvuzonse, kotero Iye akhoza kupereka chosowa chirichonse. Ndi, wodziwazonse, ndiponso amadziwa zosowa zanu, za zimene inu mukuzisowa.

11 Ine ndikumulamulira aliyense amene ine sinditha . . . ine ndakhala ndikuchita mwaliwiro mmene ine ndikanathera, ngakhale kuyambira pamene ine ndafika kuno mmawa uno, ndipo ine ndimutenga aliyense amene ine ndingathe. Ndipo ngati . . . Amene ine nditi ndiwaphonye, Mulungu wamphamvuzonse—adzapereka zosowa zanu zonse molingana ndi chuma Chake mu Ulemelero.

12 [M'bale Branham akupumira, kenako akulankhula ndi M'bale Neville—Mkonzi.] Ine ndikulephera kuwerenga zimenezo bwino bwino. Kodi inu mungawerenge izo?

Ndi cholengeza chapadera cha mtundu wina. Ndipo ine ndikuganiza Billy Paul ayenera kuti ndi yemwe walemba ichi. Kotero iye ali ngati ine; ine ndimalephera ngakhale kuwerenga zolemba zanga zomwe. Ndipo kotero ine ndiri ndi chikhukhuza changa changa. Ndipo ngati inu mutawona zina zophunzitsa zanga apa, zimene ndalemba apa, inu mukuganiza kuti mungazimvetse izo? [M'bale Branham akusonyeza zolemba za phunziro lake kwa osonkhana, ndipo iye akuseka limodzi ndi iwo—Mkonzi.] Ine ndiri ndi ngati nyenyezi, ikuwoloka mlatho, ndi zina zotero, basi zonse . . .

[M'bale Neville akuwerenga cholengeza—Mkonzi.]

M'bale Adair, Adair waku Arkansas, amuwone M'busa Pearry Green kumbuyo kwa tchalitchi pomwe pano. Chabwino.

13 Tsopano, kotero chinthu china chimene ine ndingati—ndikufuna kuti ndilengeze pano ndi—ndi chakuti, usiku uno tsopano tikhala ndi misonkhano ya machiritso. Ife tiwapempherera odwala usikuuno, ndipo kotero ine—ine ndikudalira kuti inu mudzakhala pano.

14 Ndipo ife tikutumiza moni kwa anthu onse uko kudutsa dzikoli, mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti Mulungu akudalitseni inu mmawa uno. Ena a inu muli kale masana. Uko ku New York, pakali pano ndi masana. Ndipo uko ku Arizona, Gombe la Kumadzulo, ndi seveni koloko kale. Kotero pali . . . Ndipo kuno ife tiri pakatikati. Kotero Mulungu akudalitseni inu pamene inu mukumvetsera. Tsopano ichi chikhoza kukhala . . .

Ine ndachitenga pa mtima wanga, pokhala kuno . . .

15 Ndipo ine sindimalolezedwa kuti ndikhale ndi nyumba zoyankhuliramo, ndipo potsiriza iwo anakhala ngati anatipatsa ife chilolezo; ife tikhoza kukhala ndi msonkhano umodzi, koma ife tisadzapemphereremo wodwala aliyense. Ine—ine sindikuti . . . Umenewo ndi utumiki wanga. Ine ndiyenera kuchita zimene Mzimu Woyera ukundiuza ine kuti ndichite. Kotero ine—ine ndinazikana izo, chifukwa ine ndikufuna kuti ndikhale pa ufulu wochita chirichonse chimene Mzimu Woyera ukuti ndichite. Mukuona? Kotero ine ndinaganiza ife tikhoza kungomva kuwawa tsiku limodzi lina, mulimonse, mu kachisi. Ndipo kwazizira mmawa uno. Ambuye wangotikonzera tsiku labwino ife kuno, kotero ndife othokoza.

16 Tsopano, pochita izi, ine ndabwera kuno ndi cholinga chodzaphunzitsa Miliri yotsiriza, Miliri yotsiriza Isanu ndi Iwiri, ndi Malipenga otsiriza Asanu ndi Awiri, ndi Mabingu otsiriza Asanu ndi Awiri, a Bukhu la Chivumbulutso, kuzimangirira izo pamodzi mu ora lino limene ife tsopano tikukhalamo; kuti zikatsatire kutsegula kwa Zisindikizo Zisanu ndi Ziwiri, Mibadwo Isanu ndi Iwiri. Kotero, ife timalephera kuti tipeze chipinda kuti tidzachitiremo zimenezo. Kotero ine—ndikuyembekeza kuti, mwamsanga mmene ine ndingathere, ife tidza . . . tidzatha kupeza malo okwanira a zimenezo, mwina kuno kapena mu Louisville, New Albany, kapena kudzaika tenti, kuti ife tidzangokhala motalika mmene Ambuye angatitsogolere ife kuti tichitire.

17 Koma mu ichi tsopano, ine ndinatenga mwayi uwu kuti ndifotokoze kwa anthu zokhulupirira zanga ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, ndiyeno nkukubweretsani inu ku ora limene ife tiri nkukhalamo. Ndipo potere, icho si cha munthu winawake, tizikhulupiriro, chirichonse chimene chingakhale; ndi basi mmene ine ndikuwonera Mawu a Mulungu. Ndipo Lamlungu lapitali ife tinali ndi kutsanulira kwabwino zedi kwa Mzimu

pa Mawu. Izo zinali motalika kwambiri, ndipo ine ndimadana nazo kukhala motalika chomwecho; komabe ife sitikudziwa kuti ndi nthawi yanji yomwe ife titi tidzakomane kwa nthawi yathu yotsiriza. Ndipo ife tiyenera, monga . . . tikufuna kukhala. Ine ndikufuna kukhala, kani, monga Paulo ananena wakaleyo, "Ine sindinaleke kukuuzani inu Uphungu wonse wa Mulungu." Yesu anati Iye sanawabisile kalikonse akuphunzira Ake.

Ndipo pamene ine, ndiri wotanganidwa kwambiri kuyesera kuti ndikhale pansi pa kudzoza kwa Mzimu Woyera, kuti ndipeze chimene—ora, Uthenga wa orali uli, ine nthawizina ndimalephera kuti ndituluke ndi kukachita ntchito zanga ngati wantchito wa Khristu, ngati mtumiki. Koma ine ndiri nawo amuna angapo amene amayesera kuti azindithandizira ine kuchita izi, kwa omwe ine ndiri wothokoza, abale anga onse otumikira.

18 Tsopano, ine sindimatanthauza kuti ndiziyesera kuwasunga anthu. Ngati inu, kunja uko ku dziko kumene Uthenga ukupita, mungakhoze kuima ndi kuyang'ana pozungulira tchalitchi chino mmawa uno, mu tinjira, kwa ana, kunjako, mawailesi ayatsidwa, m'mabasi, ngolo, ndi zina zotero, ndi magalimoto, inu mukhoza kuwona vuto lake. Ndiyeno msonkhano uliwonse, ambiri, ambiri akuyendetsa; ndipo akuimba, ndi zina zotero, iwo alephera kuti alowe kapena pozungulira. Ndipo ife tikusowa malo okulirapo kuti anthu adzakhoze kukhala ndi kukhala momasuka.

Ndiyeno kubweretsa—Uthenga umene ine ndikuganiza kuti ndi wofunikira kwambiri, ine ndikumverera kuti ife tiyenera kudzatero, mmodzi aliyense, adzakhale womasuka ndi wokhazikika, ndipo potero ife tikhoza kumadzamvetsera; tiri ndi mapensulo athu ndi pepala, ndi zolemba ndi Baibulo, ndi zina zotero, kuti tidzalembe—zolemba. Koma mwanjira iyi ine ndimaganiza ine ndibwerere ku nthawi imene ife tiri nayo, imene ife tiri nkukhalamo, ndi kudzayesera kuti ndibweretse zina za zinthu izi zimene inu muti mukakomane nazo. Ndipo inu muzikazisowa izo.

19 Ngati ine nditabwera kuno lero, kapena tsiku lina lirilonse, kapena mtumiki wina aliyense, kudzayesera kuti ndibweretse uthenga kwa anthu, anthu akufa monga ife tiri, ndipo nthawi ili pafupi kwambiri, monga ine ndikukhulupirira tsiku la lero; ine ndingakhale wachinyengo nditayesera kuti ndibweretse chinachake chimene ine ndikudziwa kuti chingakusangaletseni ndipo nkukhala chotsutsana ndi Mawu a Mulungu, kapena chinachake choti chikope anthu, kapena—kapena chinachake monga choncho; ine—ine sindingakhale . . . ine sindingakhale chimene ine—ine ndadzera pano kuti ndidzakhale, mtumiki wa Khristu. Ine ndikufuna kuti ndibweretse chinachake chimene ine ndikuganiza kuti ndi chofunikira kwambiri kwa inu, osati kuti basi ndidzawonedwe; koma kuganiza kuti ndi chinachake chakuti ngati ine nditafa lero, mawa icho

chidzakhala chitazikika mu mtima mwanu kuti muzipitirira ndi kumakamutumikira Mulungu.

20 Tsopano ine ndikufuna kunena kuti pali chinachake chimene chikukonzekera kuti chichitike. Ine ndikuchidziwa icho. Ambiri a inu pano mukukumbukira pamene M'bale Junior Jackson anabwera kwa ine pang'ono pokha ndisanapite ku Arizona, za loto limene iye anali nalo. Chinthu chachilendo! Ndi angati akukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Ndipo Ambuye anatipatsa ife kutanthauzira, ndipo izo zinachitika mmene zinanenedwera. Tsopano, iye walota kumene loto linanso, chinachake.

21 Ndipo chinthu chachirendo, munthu anali kuno tsiku lina, wochokera ku Oregon. Samandidziwa nkomwe ine, ndipo anali . . . analota loto lomwelo, limene Junior Jackson analota, ndipo—ndipo anabwera kudzandiuza ine. Ine—ine sindikudziwa kutanthauzira kwake; ine ndikuyembekezera Ambuye. Koma ine ndikudziwa kuti chikhala chinachake chochokera kwa Mulungu. Mungokumbukira zimenezo. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndi chinachake chimene chikubwera kuchokera kwa Mulungu. Ine sindikudziwa kuti icho ndi chiyani. Chokhudza kwenikweni, chokhudza kwambiri! Moonadi, molingana ndi—maloto omwe amuna awiriwo . . . Mmodzi wa iwo ine . . . iye akhoza kukhala wa Baptisti, Presbateria. Iye—iye mwina wakhala pano mmawa uno. Ine sindikudziwa. Iye anali kuno tsiku lina. Ine sindikumudziwa munthuyo.

22 Koma iye amanena lotolo, ali ndi misonzi mmaso mwake. Ndipo izo zinamugwedeza iye. Iye anabwera njira yonse kuchokera ku Oregon kuno, kuti adzafotokoze izo. M'bale Jackson anabwera chimodzimodzi, mmawa uno. Munthu winayo osamudziwa mzakeyo; wina, mamailosi sauzande kwa mzake, ndipo maloto onsewo ndendende basi pa chinthu chomwecho. Kotero Mzimu Woyera wandibisila ine kutanthauzira kwake. Ine sindikudziwa kuti ndimuuze chiyani munthuyo. Koma ine ndikudziwa Mulungu akukonzekera kuti achite chinachake, ndipo icho chikhala chaulemelero mmaso mwathu.

23 Tsopano, Uthenga mmawa uno, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera ku Bukhu la Agalatia. Ine sindilalikira kapena basi . . . Ili ndi phunziro la Sande sukulu. Ndipo tsopano, amuna inu ndi akazi amene mwaimirira mmakoma, ndipo wina akafuna kuti musinthane ndi kukulolani inu kuti mukhale pansi pang'ono, kapena chinachake, tsopano, inu simunditangwanitsa ine; mungokhala molemekeza basi. Ndipo ngati amayi, ana awo akamalira kapena chinachake, wina achoke kwa anako kuchitira kuti iwo akhale ndi malo a mwanayo.

24 Ndipo tsopano inu mutenge mapensulo anu, Baibulo, ndipo mukonzekere kuti muzilemba ena a Malemba amene ife titi tiwerenge. Ine sindikufuna kuti inu mumangike.

Ine ndikufuna kuti inu mumverere—ine ndikufuna kuti inu mumverere kuti muli ndi ufulu wokhala ndi kumaphunzira. Ndipo inu mukhoza kusagwirizana nazo, chimene ndi chabwino. Koma ine ndikungolankhula izi kudutsa fukoli mmawa uno, kuchitira kuti anthu amene akhulupirira Uthenga umene Ambuye Yesu andipatsa ine wa ora lino, akakhoze kudziwa chimene chikuchitika, ndi kukachiika icho mu Lemba.

25 Lamlungu lapitali ife tinalankhula za *Iwo Odzozedwawo Mu Tsiku Lotsiriza*. Ndipo ngati inu, aliyense wa inu, muli omvetsera tepi, mukhale otsimikiza kuti mukatenge tepi imeneyo. Sikuti ife tikufuna kuti tizigulitsa matepi; lingaliro lake si limenelo. Ndi lingaliro la kufalitsa Uthenga. Mukuona? Mukuona? Ngati inu muli ndi makina a tepi, mukatenge gulu la anthu pamodzi, ndipo mukaiyimbe iyo, ndipo mukamvetsere mwatcheru. "Iwo odzozedwawo."

26 Inu mumamva anthu amauka ndi kuti, "O, Baibulo linati, 'Masiku otsiriza, aneneri abodza adzauka ndipo adzachita zinthu izi.'" Ndizo ndendende Lemba. Ndiye kodi zimenezo ndi zapati? Izo ziyenera kuikidwa molondola.

Usikuuno ine ndikufuna kuti ndilankhule, ngati Ambuye alola, za: *Mulungu Akuwululidwa Mu Mawu Ake Omwe*, momwe kuti diso silingakhale pamene khutu liyenera kukhala. Mukuona? Chimodzimodzi ngati kusindikiza Baibulo lonse, ndipo, mu Baibulo lonselo, akujambula Yesu Khristu. Kotero ine ndikufuna kuti ndilankhule pa zimenezo usikuuno, Ambuye akalola. Ndipo tsopano, ngati si choncho, tsiku lina mtsogolo.

27 Tsopano mu Bukhu la Agalatia. Ndi mu Bukhu la Akorinto Wachiwiri 4:1 mpaka 6, kenako Agalatia 1:1 mpaka 4, ine ndikukhumba kuti ndiwerenge Lemba lina. Tsopano mu Agalatia 1:1 mpaka 4, "Paulo, mtumwi," muwone kuimikirako mofulumira ndithu. *Mtumwi* amatanthauza "wina wotumidwa," kapena, "mmishonare."

> *Paulo, mtumwi, (wosachokera kwa anthu, kapena wa munthu, koma . . . Yesu Khristu, ndi Mulungu Atate, amene anamuukitsa iye kwa akufa;)*
>
> *Ndi abale onse amene ali ndi ine, kwa mipingo ya ku Galatia:*
>
> *Chisomo chikhale* kwa *inu ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate* wathu*, ndi kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu,*
>
> *Amene anadzipereka yekha chifukwa cha machimo athu, kuti akatilanditse ife ku dziko loipa la pakali pano, monga mwa chifuniro cha Mulungu . . . Atate wathu*:
>
> *Kwa iye kukhale ulemelero kwa nthawi za nthawi. Ameni.*

28 Tsopano mu Bukhu la Akorinto Wachiwiri, mutu wa 4, ndipo ife tiwerenga kuyambira 1 mpaka 6, ndime.

> *Chifukwa chake popeza tiri nawo utumiki uwu, monga ife talandira chifundo, ife sitifoka ayi;*
>
> *Koma tazikana zinthu zobisika zosawona mtima, osayenda mochenjerera, kapena kuchita nawo mawu a Mulungu mwachinyengo; koma mwa mawonetseredwe a choonadi kuzivomereza tokha ku chikumbumtima cha munthu aliyense pamaso pa Mulungu.*
>
> *Koma ngati uthenga wathu ubisika,* iwo *wabisika kwa iwo amene atayika:*

Ngati zimenezo sizikubweretsamo kukonzedweratu, ine sindikudziwa kuti chingachite motero ndi chiyani.

> *Mwa amene mulungu wa dziko lino wachititsa khungu malingaliro a iwo amene sakhulupirira, kuti chiwalitsiro cha uthenga wa ulemelero wa Khristu, amene ali chithunzithunzi cha Mulungu, chiwalire pa iwo.*

Chimodzimodzi monga izo zinali mmunda wa Edeni, "Anawaika iwo, kuwopa kuti iwo angawukhudze Mtengo umenewo."

> *Pakuti ife sitilalikira osati za ife tokha, koma Khristu Yesu Ambuye; . . . ifeeni antchito anu chifukwa cha* Khristu.
>
> *Pakuti Mulungu, amene analamulira kuwala kuti kuwale mu mdima, kwawalira mmitima mwathu,* ndi *kutipatsa kuwala kwa chidziwitso cha ulemelero wa Mulungu pa nkhope ya Yesu Khristu.*

29 Ameni! Chomwecho akuwerengeka Mawu! Tsopano, phunziro langa mmawa uno, ndiro: *Mulungu Wa M'badwo Woipa Uno*. Monga ife tawerengera mu Malemba, "mulungu wa dziko lino, m'badwo woipa uno." Tsopano, Uthenga uwu ukuloza zoipa za m'badwo woipa uno, ndipo iwo ukukwanira ku ulosi wa m'badwo woipa uno.

Ndipo ndikukhulupirira kuti aliyense . . . kuti Baibulo liri nalo yankho lirilonse la m'badwo uliwonse, linalembedwa kale mu Baibulo, la wokhulupirira wa m'badwo umenewo. Ine ndikukhulupirira kuti chirichonse chimene ife timachisowa chinalembedwa momwemu *Umu*, zikungosowa kuti zitanthauziridwe ndi Mzimu Woyera. Ine sindikukhulupirira kuti munthu aliyense pa dziko lapansi ali nawo ufulu woika kutanthauzira kwake kwake ku Mawu. Mulungu samasowa aliyense kuti atanthauzire Mawu Ake. Iye ndi Wodzitanthauzira Iye Mwini. Iye anati Iye akanadzachita izo, ndipo Iye akuzichita izo.

30 Monga ine ndanenapo nthawi zambiri. Iye anati, "Namwali adzaima," Iye analankhula zimenezo kudzera mmilomo ya mneneri, ndipo iye anatero. Palibe aliyense ayenera kutanthauzira zimenezo. Pachiyambi, Iye anati, "Kuwale," ndipo zinachitika. Palibe amene ayenera kutanthauzira Izo. Iye anati, "Mu masiku otsiriza, Iye adzatsanulira Mzimu Wake pa mnofu wonse," ndipo Iye anatero. Izo sizikusowa aliyense kuti atanthauzire Izo. Iye anati, "Mu masiku otsiriza, zinthu izi" (zimene ife tikuziwona zikuchitika tsopano) "zidzakhala pano." Izo sizikusowa kutanthauzira kulikonse. Izo zinatanthauziridwa kale. Mukuona?

31 Tsopano, zindikirani mwatcheru tsopano pamene ife tikuphunzira Mawu. *Mulungu Wa M'badwo Woipa Uno*, umene ife tiri kukhalamo. Zikhoza kuwoneka zachirendo, chinthu chachirendo kwambiri, mu m'badwo uno wachisomo, pamene, "Mulungu akuwatenga anthu chifukwa cha Dzina Lake," ameneyo ndi Mkwatibwi Wake, mu m'badwo woipa uno umene uyenera kutchedwa m'badwo wa zoipa. M'badwo kumene umene "Mulungu akuwaitana anthu chifukwa cha Dzina Lake," mwa chisomo, atuluke, ndipo ukutchedwa m'badwo woipa. Tsopano, ife titsimikizira mwa Baibulo kuti uno ndi m'badwo umene Iye anali kuwukambawo. Chinthu chachirendo kwambiri kuti uchiganizire, kuti mu m'badwo woipa wonga uwu, kuti Mulungu ndiye angakhale akumuitana Mkwatibwi Wake.

32 Inu mukuzindikira, Iye anati, "anthu," osati "mpingo." Bwanji? Komabe, Iwo ukutchedwa Mpingo, koma Iye akanadzaitana "anthu." Tsopano, mpingo ndi kusonkhana kwa anthu ambiri a mapangidwe onse osiyanasiyana. Koma Mulungu akumuitana mmodzi apa. . .Iye sanati, "Ine ndidzawaitana a Methodisti, Baptisti, Pentekoste." Iye anati Iye adzawaitana anthu. A chiyani? A Dzina Lake. Mwaona, anthu; mmodzi kuchokera ku Methodisti, mmodzi kuchokera ku Baptisti, mmodzi kuchokera ku Lutheran, mmodzi kuchokera ku Katolika. Mukuona?

Koma Iye akuitana, osati gulu la mpingo, koma "anthu chifukwa cha Dzina Lake," amene akulandira Dzina Lake, otomeredwa mu Dzina Lake, akupita ku chikwati kuti akakwatiwe ndi Iye, kuti akakhale gawo la Iye, mwaona, mwa kukonzedweratu. Chimodzimodzi monga mwamuna amene amasankha mkazi woyenera mu moyo, anadzozedweratu kuti adzakhale gawo la thupi lake. Kotero, zimenezo ndizo, Mkwatibwi wa Khristu adzakhala, ndipo alipo tsopano, kuchokera kale, anadzozedwa ndi Mulungu kuti adzakhale gawo la Thupi limenelo. Mukuona? O, Malemba ndi olemera kwambiri, odzaza uchi!

33 Zindikirani, osati zimene winawake wanena, zimene winawake waziitana; koma zimene Mulungu anazisankha asanaikidwe maziko a dziko lapansi, ndipo akuwaitana anthu

awa mmasiku otsiriza; osati bungwe. "Anthu chifukwa cha Dzina Lake." Ndipo m'badwo woipa uno ndi pamene Iye akuchita izo, m'badwo uno kumene wa chinyengo.

34 Sabata yathayi, mu Mateyu 24, iwo unali m'badwo wachinyengo kwambiri wa mibadwo yonse. Mibadwo yonse ya chinyengo, kuyambira mmunda wa Edeni, njira yonse mpaka mmusi, sipanayambe pakhalapo m'badwo wachinyengo kwambiri ngati m'badwo uno. "Aneneri abodza adzauka ndipo adzasonyeza zizindikiro ndi zodabwitsa, ngati nkotheka kuti akanyenge Osankhidwa omwe." Mukuona? Tsopano, mipingo yozizira basi, yofunda, yokhuthara, ndi zina zotero, ya mbalume zopangidwa ndi anthu, zomwe sizingakhale; Wosankhidwa sadzapereka tcheru chirichonse kwa izo. Koma ziri kumeneko pafupifupi ngati chinthu chenichenicho. Kungowasiya Mawu amodzi ndi zonse zimene inu muyenera kuchita. Zolonjezedwera m'badwo; nthawi yopambana zedi! Akhristu, konsekonse, musamalitse ora limene ife tiri nkukhalamo! Mulembe, ndipo mukawerenge, ndipo mukamvetsere mwatcheru.

35 Kodi Mulungu akuwaitaniranji anthu atuluke mu m'badwo woipa uno, a Dzina Lake? Chifukwa chake ndi chakuti, kuti amuyese Iye, Mkwatibwi Wake. Ndikuti . . . Pamene Iye akuwonetseredwa, akuyesedwa, akutsimikiziridwa, akutsimikiziridwa kwa Satana. Monga izo zinali pachiyambi, chomwecho izo zidzakhala pamathero.

36 Monga mbewu imayambira mu nthaka, iyo imabwera kudzera mwa zotengera, moyo wa iyo, koma iyo imadzatsirizira kukhala mbewu yomweyo mmene iyo inaliri pamene iyo inkapita mu nthaka.

Ndipo mwanjira yomweyo mbewu yachinyengo inagwera mu nthaka, mu Edeni, ndipo mwanjira yomweyo ikudzathera mu masiku otsiriza.

Chimodzimodzi basi monga mmene Uthenga unali pamene iwo unadzagwera kwa chipembedzo ku Nicaea, Roma, iwo ukudzathera mu bungwe lapamwamba.

Chimodzimodzi basi monga Mbewu ya Mpingo inagwera kumbuyo uko, ndi zizindikiro, zodabwitsa, ndi Khristu wamoyo pakati pawo, iyo ikudzathera mu masiku otsiriza pansi pa utumiki wa Malaki 4, ndi kudzabwezeretsanso Chikhulupiriro chapachiyambi chimene chinaperekedwa kamodzi.

37 Ife tikupeza tsopano, m'badwo woipa uno uli wakuti udzatsimikizire, kwa Satana, Iye sali monga Eva, kuti Iye sali monga mkazi wa mtundu umenewo. Ndipo Iye adzayesedwa ndi Mawu Ake, Mkwatibwi, monga mkwatibwi wa Adamu anayesedwa ndi Mawu. Ndipo mkwatibwi wa Adamu anakhulupirira chidutswa chirichonse cha Mawu, onse, koma anasokonezeka pa lonjezo limodzi, lakuti, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," lero, mwaona; koma

analephera pa lonjezo limodzi, pansi pa yesero la mdani, maso ndi maso. Ndipo tsopano, anthu amene akuitanidwira Dzina Lake, zoona, ali Mkwatibwi Wake. Iye ayenera kukomanizana nacho chinthu chomwecho; osati kokha mwa choonadi cha chipembedzo kapena chinachake, koma Mawu aliwonse!

38 Pakuti, pachiyambi cha Baibulo, munthu anapatsidwa Mawu a Mulungu kuti azikhala nawo moyo. Mawu amodzi, atatanthauziridwa molakwika ndi—munthu wotchedwa Satana, mwa munthu wa chinyama wotchedwa serpenti. Satana, mwa munthu uyu, amakhoza kulankhula ndi Eva, ndipo anatanthauzira molakwika Mawu kwa iye, ndipo anataika. Mwaona, Izo ziyenera kukhala Mawu aliwonse.

39 Pakati pa Baibulo, Yesu anabwera ndipo anati, "Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse," pamene Iye anadzayesedwa ndi Satana.

Tsopano, Mulungu akutiuza ife kuno mu masiku otsiriza, kuti, "Mulungu wa dziko lino adzauka mu masiku otsiriza."

"Ndipo aliyense amene adzawonjezera mawu amodzi kwa Iwo, kapena kudzachotsamo Mawu amodzi kwa Iwo, gawo lake lidzachotsedwa kuchokera mu Bukhu la Moyo."

Mulungu atichitire ife chifundo! Ndipo asatilole ife kuti tiziyenda ngati malaya okhuthara, zidali panja, mutu mmwamba, odziwa zonse, pakuti ife nafenso nthawi ina tinali mu kusamvera. Tiyeni ife ndi chisomo, ndi chifundo, ndi kukhudzidwa mu mtima mwathu kwa Mulungu, modzichepetsa tizifika ku Mpando wa chisomo.

40 Zachirendo tsopano, patadutsa zaka zina naintini handiredi za kulalikira Uthenga, ndipo tsopano iye, kameneko ndi kachitidwe ka chidziko, ndi koipa kwambiri kuposa mu masiku pamene izo, pamene Iye anali kuno. Kachitidwe ka kachidziko ndi koipa kwambiri. Dziko lalunjika ku mapeto aakulu. Inu mukudziwa zimenezo. Ambuye akukwaniritsa Mawu Ake ponseponse.

41 Dzulo, nditaima . . . ine ndikuyembekeza kamunthu kakang'onoko sikati . . . Iye satero. Ine ndinali nditabwera ndi mkazi wanga, ndi Akazi a Woods, M'bale Roy Roberson, kwinakwake kuno, M'bale Woods, ife tinali titaima kuno ku Youngstown Shopping Center yaing'ono iyi, kuti ndikagule—kaphukusi kamene Mlongo Woods anali nako. Ndipo pa . . . pamene ife tinali titaima pamenepo, mnyamata wachichepere anabwera ndipo anadzidziwitsa yekha, ndipo mlendo kwa ine. Mnyamata winanso anabwera ndipo anati iwo anali kuchokera ku Alabama, Georg- . . . ine ndikukhulupirira Georgia, chifukwa ine ndinawafunsa iwo ngati amamudziwa M'bale wathu Welch Evans. Ndipo ife tinalankhulana maminiti pang'ono. Ndipo pamene ine ndinapita kuti ndizinyamuka, mnyamata uyu anayang'ana pa ine. Pamene mnyamata winayo ndi mwana

wawo wamng'ono amachokapo, mnyamata uyu anandiyang'ana ine. Iye anati, "Chinthu chimodzi chokha chimene ine ndikufuna kuti ndinene."

Ine ndinati, "Kodi—kodi ndinu wokhulupirira? Kodi ndinu Mkhristu?

Anati, "Ayi, bwana." Iye anati, "Ine nda . . ."

42 Ine mwinamwake sindibwereza basi mawu amene iye ananena apa, koma iye mwinamwake anali wotsutsa pang'ono. Ine ndinali nditamufunsa iye za zinthu za Mngelo wa Ambuye akuwonekera. Ndipo iye anati iye anali atamva za izo, koma iye anali asanapiteko ku tchalitchi nkale lomwe, tchalitchi chino. Ine ndinati, "Kodi iwe ukukhulupirira Izo?"

Anati, "Inde, bwana." Iye anati, "Ine—ine ndakhala ndikupenyerera chinachake." Anati, "Anthu akhala akundiuza ine za zoneneratu izi ndi zinthu, ndipo ine ndinamva pa tepi kuti inu munaneneratu momwe California adzang'alukire monga choncho." Ndipo anati, "Pamene ine ndinawona izo mu pepala, ndiye ine ndinakhulupirira izo." Iye anati, "Ine ndikubwera lero kapena mawa," limenelo ndi lero, "kwa nthawi yanga yoyamba."

Ine ndinati, "Ambuye akudalitse iwe, mwana," ndipo ndinayamba kugwira chanza dzanja lake.

Iye anati, "Koma ine ndikufuna kuti ndinene chinachake kwa inu, bwana." Iye anati, "Ndine wotayika wotayika basi momwe ndingakhalire." Iye anati, "Ine ndiri ngati ndalama ya chitsulo pa mulu wa mchenga, itataika!"

43 Ine ndinati, "Koma iwe sukusowa kuti ukhale mwanjira imeneyo. Alipo winawake yemwe waima pakali pano Yemwe angathe kukupeza iwe miniti imene iwe wakonzeka kuti upezeke."

Iye anati, "Ndine wokonzeka."

Ine ndinati, "Kodi iwe ungaweramitse mutu wako?"

Iye anati, "Ine sindikuchita manyazi."

Osati zokhazo ayi, koma iye anagwada pa mawondo ake, uko pa bwalo loimika magalimoto ilo, pamaso pa anthu onse. Anthu mu msewu akumuwona iye. Pamenepo ife tinamupempherera iye, mpaka iye anapereka mtima wake kwa Mulungu. Iye anabwera ali, wochimwa; anabwererako, ali mwana wa Mulungu. Iye anadzera kumbali ya galimotoyo, wakufa; ndipo anabwererako ali, wamoyo.

44 Ine ndinati, "Dziwe lidzakhala lotsegula mawa."

Kuli kasupe wodzadza Magazi,
Wotuluka kuchokera mmisempha ya Emanuele,
Mmene ochimwa akamizidwa pansi pamafundewo,
Amataya litsiro la zowatsutsa zawo.

Ine ndinati, "Dzuka ndipo ukabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, ukuitanira pa Dzina la Ambuye. Mulungu akudzadza iwe ndi Mzimu Woyera, ndipo akupatsa iwe zinthu zazikulu izi, ndipo akupanga iwe kuti ukhoze kuziwona Izo."

45 Ndi chiyani chimenecho? Dziko likulunjika ku mapeto. Bwanji? Mzimu wa kulekelela, kuvunda kwa makhalidwe, chipembedzo cha sayansi, zatsogolera izo waku "mphanga ya mbalame zirizonse zodanidwa ndi zosayera," monga Baibulo limanenera. Tiyeni tiwerenge izo, Chivumbulutso 18. Basi pamene ife tikuyambitsa mfundo iyi, ife tipeze Chivumbulutso 18:1 mpaka 5. Ine ndikuganiza ine ndalemba zimenezo molondola.

> *Ndipo zitatha zinthu izi ine ndinawona mngelo wina akutsika kuchokera mmwamba, wakukhala nawo ulamuliro wamphamvu; ndipo dziko linaunikiridwa ndi ulemelero wake.*
>
> *Ndipo anafuula ndi mawu olimba,* (tsopano anthu inu amene munali ndi maloto)*. . .akuti, Babulo wamkulu* akugwa, *ali* kugwa, *ndipo wasandulika mokhalamo ziwanda, ndi mosungiramo mzimu uliwonse wonyansa,. . .chisa cha mbalame iliyonse yonyansa ndi yodanidwa.*
>
> *Chifukwa mafuko onse* aledzera *vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake* (mpingo) ziwerewere, *ndi mafumu a dziko lapansi achita naye* ziwerewere, *ndipo ochita malonda a mdziko alemera ndi mphamvu ya kudyerera kwake.*
>
> *Ndipo ine ndinamva liwu lina kuchokera kumwamba, likuti, Turukani mwa iye, anthu anga, kuti* inu *musakhale otenga nawo a machimo ake,. . .kuti* inu *musalandire za miliri yake.*
>
> *Pakuti* tchimo *lake lafikira mmwamba, ndipo Mulungu* akukumbukira kusaeruzika *kwake.*

46 Ndi chenjezo bwanji! Zimenezo zikuwuponyera mpingo ndendende mmbuyo ku Chivumbulutso 3:14, mpaka ku m'badwo wa Laodikaya, wolekerera; wachipembedzo kwenikweni, koma wolekerera. "Iwe, chifukwa iwe unena kuti, 'Ife tiri olemera, sitisowa kanthu,' iwe sukudziwa kuti ndiwe wamaliseche, womvetsa chisoni, wakhungu, ndipo sukudziwa izo ayi." Mwangwiro ndi Lemba la m'badwo uno, osati Lemba la m'badwo

wa Daniele, osati iwo a dzina la . . . m'badwo wa Nowa, koma mu m'badwo wotsiriza uno, woipa.

47 Zindikirani apa, "Iwe uli wamaliseche." Mulole zimenezo zilowerere mwakuya kwenikweni. Ine ndikudziwa ndikhoza kukhala ndi kusagwirizana kochuluka pa lingaliro ili, koma zafika pamalo akuti Mkhristu sizingatheke kutuluka mnyumba yake ndipo nkusabweretsedwa mu kukhalapo kwa m'badwo woipa uno, ndi akazi ovala mosakwanira.

48 Akazi, ine ndinena izi, ndipo ine ndikufuna kuti inu mumvetsere. Ndipo, amuna ndi akazi, inu mukhoza kutsutsana nazo izi, koma ine ndikumverera kutsogozedwa kuti ndinene izi. Kodi inu mukudziwa, mkazi aliyense yemwe amadzivula yekha monga choncho mutu wake sukuyenda bwino? Kodi inu mukudziwa, iye ali, kaya iye akhulupirira izo kapena ayi, kapena sakuganiza chomwecho, iye ndi wachiwerewere? Ngakhale mkaziyo akhoza kuima ndi dzanja lake pamaso pa Mulungu ndi kulumbirira kuti iye sanayambe wakhudzidwapo ndi mwamuna aliyense koma mwamuna wake, ndipo izo zikhoza kukhala zoona zenizeni, komabe iye ndi wachiwerewere. Yesu anati, "Aliyense amene ayang'ana pa mkazi namukhumba iye wachita naye kale chigololo." Ndipo mkaziyo akhoza kukhala . . .

49 Taonani, iye ali "wamaliseche," Baibulo linatero, "ndipo sakudziwa izo ayi." Mzimu umene ukumudzoza iye kuti azichita zoterozo ndi woipa, mzimu wachiwerewere. Mawonekedwe ake akunjaku, thupi lake, mnofu wake, iye akhoza kukhala woyera. Iye akhoza kusamachita chigololo chirichonse, ndipo akhoza kulumbira kwa Mulungu ndipo nkukhala zoona, kuti iye sanateropo, koma mzimu wake ndi mzimu wachiwerewere. Iye wachititsidwa khungu kwambiri ndi mulungu wa dziko lino wa fashoni; iye wadziveka yekha mwachigololo ndipo akumapita kunja uko.

50 Tsiku lina, M'bale Woods ndi ine tinali kuika ngalawa yathu mu mtsinje. Ine ndinali woti ndichoka pa nyumba kwa maminiti pang'ono, kuti ndipite ku mtsinje uko. Ndipo kulikonse kumene iwe umapita, akazi okhala ndi milu iyi ya . . . zotchedwa akabudula kapena chinachake, atazikulungiza pa iwo. Chimenecho ndi chamanyazi. Mkazi sangakhale wa malingaliro ake abwinobwino ndipo nkumavala chirichonse chonga zimenezo. Iye wadzadzidwa ndi mzimu wachiwerewere. Tsopano, inu mudzathana zimenezo ndi Mulungu, dona, chifukwa inu mudzapeza tsiku lina kuti zimenezo ndi Zoona.

51 Inu mumakwanitsa bwanji, dona, mukudziwa momwe thupi lanu liri lopatulikira, ndipo nkumaliwonetsa ilo kunja uko kwa osilira awa, adierekezi ochimwa amene akuyenda mu msewu wa lero? Ngati ana aamuna a Mulungu akadakhala onse ana aamuna a Mulungu, amuna anu akadakhala mwana wa Mulungu, iwo mwina akadakupangani inu kuti muzivala zovala kapena

akadakusiyani inu. Ngati mnyamatayo akadakhala mwana wa Mulungu, iye sakadakwatira chinthu choterocho. Mukuona?

Inu mukuti, "Inu mukupa-. . . " Ayi.

Ine ndikukuuzani inu Choonadi, ndipo tsiku lina inu mudzakakomana nacho Icho. "Wamaliseche, wachigololo; osadziwa izo ayi."

52 "O, ine ndikulumbira kuti ine sindinaswepo malumbiriro a mwamuna wanga." Amuna anu adzakuweruzani inu chifukwa cha izo ngati inu mukanachita. Koma Mulungu adzakuweruzani inu chifukwa cha mzimu umene inu muli nawo; osati kukuweruzani inu chifukwa cha thupi lanu, koma chifukwa cha mzimu wanuwo, munthu wamkatiyo.

53 Munthu wakunjayu ndi chinthu chogwirika chimene chimalamuliridwa ndi zokhudzira zisanu ndi chimodzi. . . kapena zokhudzira zisanu, kani. Munthu wamkatiyo ndi munthu wauzimu amene amalamuliridwa ndi zokhudzira zisanu; chikumbumtima, ndi chikondi, ndi zina zotero. Munthu wakunjayu; kuwona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, kumva.

Koma mkati mwa mzimu umenewo muli solo, ndipo iyo imalamuliridwa ndi chinthu chimodzi, kufuna kwanu. Inu mukhoza kuvomereza zimene mdierekezi akunena kapena kuvomereza zimene Mulungu akunena. Ndipo zimenezo zidzatengera mzimu umene uli mmenemo. Ngati iwo uli Mzimu wa Mulungu, Iwo uzidzadya pa zinthu za Mulungu, ndipo Iwo sudzadya pa chirichonse cha mdziko. Yesu anati, "Ngati inu mulikonda dziko kapena zinthu za mdziko, ndi chifukwa chakuti chikondi cha Mulungu sichinalowe nkomwe mu gawo la mkatili." Satana wakunyengani inu. "Ndipo munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse otuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu."

Zindikirani tsopano, ife tikupeza kuti iye ali "wamaliseche," wachisembwere ndi wambulanda.

54 Ndipo dziko likuwoneka kuti liri mu m'badwo woipa kwambiri umene unayamba wakhalapo. Palibepo mu m'badwo uliwonse mmene akazi anayamba achitapo monga choncho, ayi nkomwe koma basi chisanachitike chigumula cha dziko. Ndipo Yesu analozera kwa izo. Ife tifika kwa izo pakapita kanthawi.

55 Kodi Mulungu wataya ulamuliro, kapena kodi Iye akungololeza nthumwi ina kuti ilamulire? Ine ndikudabwa. Yankho loona kwa funso ili ndiro, mwa kulingalira kwanga, ilipo mizimu iwiri yotsutsa mu dziko lero, imene ikugwira ntchito. Tsopano, sipangakhalenso yoposa iwiri, mitu iwiri. Ndipo Umodzi wa iyo ndi Mzimu Woyera ukugwira ntchito; umodzi winawo ndi mzimu wa mdierekezi, ndipo, mu masiku otsiriza ano, mu chinyengo.

Tsopano ine ndikhazikitsa malingaliro anga pomwe apa kwa phunziro lonseli, wonsewu . . . Uthenga wathu.

56 Mizimu iwiri. Umodzi wa iyo, Mzimu Woyera wa Mulungu; winawo, mzimu wa mdierekezi, ukugwira ntchito mwa chinyengo. Anthu a padziko lapansi tsopano akupanga kusankha kwawo.

Mzimu Woyera uli pano ukuitanira Mkwatibwi kwa Khristu. Iye akuzichita izo pa kuwatsimikizira Mawu Ake a lonjezo kwa Iye, a m'badwo uno, kusonyezera kuti Iwo ndi Khristu.

Ngati chala chiyenera kuti chisunthe mu m'badwo uno, chalacho chisuntha. Ngati phazi liyenera kuti lisunthe mu m'badwo uno, phazilo lisuntha. Ngati diso liyenera kuti lipenye mu m'badwo uno, disolo lipenya. Mukuona?

Mzimu wa Mulungu, pamene Iwo wakula kukhala thunthu lamphumphu la Mulungu, ndiwo m'badwo umene ife tiri kukhalamo tsopano. Mzimu Woyera uli pano ukutsimikizira Uthenga wa orali. Ndipo Mzimu Woyera ukuchita zimenezi, kuti anthu amene akumukhulupirira Mulungu aitanidwe atuluke kuchoka mu chisokonezeko ichi.

Mzimu wosayera wa mdierekezi uli pano ukuitana mpingo wake mwa kulakwitsa, mwanthawizonse, mwa kupotoza kwa Mawu a Mulungu, monga iye anachitira pachiyambi. Mukuziwona izo zikubweranso kudzafika ku nthawi ya mbewu iyo kachiwiri, kuchokera ku Edeni? Ndi izi apa kachiwiri.

57 Tsopano, mmbuyo kudutsa kumeneko, inu muli-. . . mmibadwo inayo, inu munali a zipembedzo, inu munali a *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*. Chinachitika chiyani ndi phesi la chipembedzo? Ilo linauma. Mzimu ukumachokabe ndi kumapitirira, ndipo Iwo ukukathera mu Mbewu. Inu mukuona?

58 Ndipo mayesero, a zonsezo, akubwerera mmbuyo mwanjira yomweyo izo zinali pachiyambi. Zindikirani. Musati—musati, ayi, musaiwale izo tsopano.

Monga Yohane, Yohane Woyamba 4:5 ndi 6, ngati inu mukufuna kuti mulembe izo, iye akuikamo iwo, "mzimu wa kulakwitsa."

Eva sanangochokapo mophweka, mwakufuna, ndikuti, "ine sindikumukhulupirira Mulungu." Ayi. Kunali kulakwitsa kumene iye anakukhulupirira.

59 Satana sanatulukire poyera ndikuti, "O, chabwino, amenewo si Mawu a Mulungu nkomwe." Iye anavomereza kuti Iwo anali Mawu a Mulungu, koma iye anaikako kutanthauzira kwake kwake kwa Iwo. Chimene, Mulungu mwapoyera anawauza iwo kuti asachite.

Kodi ichi chikuchita chiyani? "Icho chikupanga chosocheretsa champhamvu, kuti anthu akhulupirire bodza, ndipo nkudzawonongedwa nalo ilo." Tsopano ngati inu

mukufuna kuti muwerenge zimenezo, Atesalonika Wachiwiri 2:11.

60 Pamene ine ndiri ndi pafupifupi, Malemba pang'ono ndithu apa, ndipo ife sitikwanitsa kuti tiwawerenge onsewo. Limodzi tsopano ndipo kenako, ine ndikupatsani inu iwo. Mmene zikuwonekera zachilendo, kuti inu mukuzifunsa izo kapena chinachake, ndipo ife tikhoza kulemba izo ndi kuwerenga kwa—kwa ubwino wanu.

61 "Kupanga chosocheretsa champhamvu," monga Baibulo linati izo zikanadzachitira, Atesalonika Wachiwiri. "Tsopano, munthu uyu wa tchimo adzabwera powonekera, ndipo adzakhala mu kachisi wa Mulungu, nkumadziwonetsera yekha kuti ndi Mulungu, ndi kuwapangitsa anthu kuti apite mu chosocheretsa champhamvu, kuti akakhulupirire bodza; ndi, kulikhulupirira ilo, nkudzawonongedwa nalo ilo."

Ndicho chinthu chomwecho chimene iye anachita kwa Eva. Anamupatsa iye. . . Sanati—sanamuuze konse iye kuti Mawuwo anali olakwika, koma anamupatsa iye chosocheretsa champhavu, mwakuti iye anakhulupirira bodza.

62 Mzimu wa chosocheretsa ndi wa mdierekezi. "Adierekezi tsopano akugwira ntchito mwa ana akusamvera." Osamvera kwa chiani? Kodi ana a lero ndi osamvera kwa chiani? Monga Eva anali, pachiyambi, Mawu owona a Mulungu. Izo nzoona. Tsopano ngati inu mukufuna kuti mumvetse izo . . .

Tiyeni titembenuzire kwa izo, Aefeso 2, miniti chabe, chifukwa zikuwoneka zabwino kuti ife. . . Ine ndiima miniti chabe, ngati inu simuli mu liwiro lalikulu, ndipo tiwerenge zina za izi. Aefeso 2:1 mpaka 2.

> *Ndipo inu iye wakufulumizitsani, amene* nthawiina *munali akufa mu kulakwitsa ndi* tchimo:
>
> *Momwe mu* nthawi *zakale munkayenda molingana ndi dziko lino, molingana ndi kalonga wa mphamvu za mumlengalenga, mzimu umene tsopano ukugwira ntchito mwa ana a kusamvera:*

63 "Ana a kusamvera." Ndipo ngati wotsutsakhristu, kuyambira uko mu ubwana wa kusamvera, kodi zidzakhala chiyani pamene izo zikufika mwa munthu wa wotsutsakhristu? Zidzakhala zonyenga bwanji! Ndi kunyenga kwamphamvu kochuluka bwanji kumene—wamkulu adzapereke kwa dziko, kuposa mwana wa khanda! Ndipo iye anati, "Mzimu wa—wa chosocheretsa tsopano ukugwira ntchito mwa ana a kusamvera," kusamvera ku Mawu. Zindikirani. Tsopano ine ndikufuna kuti ndikhazikike pa izi miniti chabe, "ana a kusamvera," mwana.

64 Kodi inu mumadziwa, inu, chiyambi chanu, ine ndikhoza kutsimikizira mwa Mawu a Mulungu kuti inu, munthu aliyense muno, anali wamoyo mwa agogo a agogo anu aamuna. Ndipo

agogo a agogo anu, inu munatulukira kwa agogo anu aamuna, kenako kwa abambo anu, ndipo kenako kwa inu. Inu mukudziwa zimenezo?

Baibulo linati, ine ndikukhulupirira ndi Ahebri 7, kuti, Melkizedeki, pamene Abrahamu ankabwera kuchokera kokapha mafumu, "Abrahamu anampatsa Melkizedeki chakhumi cha chuma chonse." Ndipo ndi uyu Paulo apa akulankhula tsopano, akuti, "Levi, yemwe analandira zakhumi, anali akadali . . . Iye anapereka zakhumi, pakuti iye anali akadali mchiuno cha Abrahamu pamene iye anakomana ndi Melkizedeki." Kotero chirichonse chimene Abrahamu amachita, ndiye ife tikupeza kuti Levi anali panthawi imeneyo mwa Abrahamu, yemwe anali agogo a gogo ake. Abrahamu anabala Isaki; Isaki anabala Yakobo; Yakobo anabala mbadwa, Levi.

Tsopano, ndiye, inu mukuona, apa pakubwera powonekera mwangwiro, kukonzedweratu.

65 Tsopano, mu Mauthenga awa, ine ndikufuna kuti—kuti—kuti nditsimikizire zinthu zimene ine ndakuuzani inu mu Uthenga, za Kuwala kwa madzulo uku kumene Mulungu anati kudzabwera pa dziko lapansi.

66 Ndipo zindikirani, ndiye, "Chirombo chimene chinali choti chidzabwera pa dziko lapansi, chidzanyenga onse amene maina awo sanalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, wophedwa asanaikidwe maziko a dziko lapansi."

67 Mu kuganiza kwake komwe kwa Mulungu; Mulungu, Mzimu wawukulu. Pachiyambi, kusanakhale konse chiyambi, Iye anali Mulungu, ndipo kodi inu mumadziwa inu munali mwa Iye nthawi imeneyo? Ngati inu muli Mkhristu tsopano, inu munali mwa Iye nthawi imeneyo.

Ndiyeno, ngati izo ziri chomwecho, Umulungu wonse mthupi unawumbidwa mwa Munthu wa Yesu Khristu. Ndiyeno pamene Yesu anafa pa mtanda, ine ndinafa limodzi ndi Iye, pakuti ine ndinali mwa Iye nthawi imeneyo; pakuti Iye anali chidzalo cha Mawu, akuwonetseredwa, podziwa kuti tikanadzawonetseredwa mtsogolomo. Ndipo ife tinali pa Kalvare limodzi ndi Iye. Ife tinakalowa mmanda limodzi ndi Iye. Ndipo ife tinawuka limodzi ndi Iye ndi chiukitsiro Chake. Ndipo tsopano ife takwera, ndi Mzimu Wake, tapita ku Mpandowachifumu wa chisomo, tikukhala limodzi mu malo a Mmwambamwamba mwa Khristu Yesu. Nthawizonse!

68 Pakuti monga nyongolosi ya moyo wachirengedwe imaikidwa pansi, kumeretsedwa kuchokera kwa bambo kupita kwa bambo, kupita kwa bambo, kupita kwa bambo, chomwechonso Moyo wa Khristu umameretsedwa.

Ndi chifukwa chake Mulungu akuwugwiritsa ntchito Mzimu wa Eliya nthawi zisanu zosiyana. Ndi chiani chimenecho? Ndiko kusiyirana.

69 Chimodzimodzi monga moyo wanu wachibadwa ndi zikhalidwe zimaperekedwa kuchokera ku kubadwa kwachibadwa kwa bambo, chomwechonso uli Mzimu wa Mulungu, umene unakonzedweratu asanakhazikitsidwe maziko a dziko.

Ndipo pamene Mawu onse a Mulungu, mwathunthu, anadzakhala mu thupi la munthu wotchedwa Yesu Khristu, mmenemo Mulungu anandipanga ine kuti ndilipire machimo anga, mwa Iye kumeneko. Zitatero Iye anandidzutsa ine, anandidzutsa ine limodzi ndi Iye, mu chiukitsiro. Ndipo tsopano ife tikukhala limodzi ndi Iye, ndi mphamvu ndi ulamuliro pa mdierekezi aliyense. O, ngati inu mutangokhulupirira zimene Mulungu wapereka! Koma ngati inu kunalibeko kumeneko, inu mulibe icho. Ndipo ngati inu mwakhala kumeneko, ndipo simukukhulupirira izo, ndipo mukuwopa kuti musunthe, inu simudzagwiritsa ntchito izo nkomwe. Koma ngati inu munali kumeneko, inu mudzagwiritsa ntchito izo, pakuti ndinu odzozedweratu kuti mudzachite zimene inu mukuchitazo.

70 "Farao," kumbali inayo, "anawukitsidwa kwa cholinga ichi," Baibulo linatero, kuti adzakhale Farao. "Yudasi Isikarioti anawukitsidwa kuti adzakhale mwana wa chitaiko."

Tsopano zindikirani Zoonadi zazikulu izi zimene ife tikuziyandikira.

71 Tsopano ife tikuwona kuti mpingo unakana kuti uwalandire Mawu a Mulungu kuti azilamulira pa iwo, ndipo unalandira Barabasi mmalo mwake. Tsopano, ngati inu mukufuna Lemba pa zimenezo, ndi Mateyu 27:15 mpaka 23. Kodi ichi chinachita chiyani? Ndi malo ati amene ichi chinachita? Tsopano taganizani za zimenezo. Pamene mpingo wa dziko, mu moyo wake wa chirungamo chachibungwe, amuna oyera, monga mmene iwo ankaganizira kuti iwo anali, ndipo anali mmaso a anthu, iwo anamupachika Yesu, ndipo anati, "Ife sitikufuna kuti Munthu uyu azitilamulira ife." Ndipo Yesu anali chidzalo cha Mawu a Mulungu. Yohane Woyamba 1, amafotokoza zimenezo. Ndipo iwo anati, "Ife sitikufuna kuti Mawu awa a Mulungu azitilamulira ife." Komabe, Iye anali Mawu, koma maso awo anachititsidwa khungu kwa chimene Iye anali. Pakuti Iye anali yankho lolunjika kwa ulosi uliwonse umene unali nkudza mwa Iye.

Tsopano, ife tonse tikukhulupirira zimenezo, chifukwa ife tikuyang'ana mmbuyo kuti tiziwone izo zikuchitika. Koma ngati dziko lingatero, zimenezo ndi pakali pano, m'bawo woipa uwu wa pakali pano, zimenezo zikadakhala kumbuyo uko pa nthawi imeneyo, iwo akanachita chinthu chomwe chomwecho chimene iwo akuchita lero, chifukwa zikadali panobe Mawu omwewo, a m'badwo uno, akuwonetseredwa. Iye adzachita zimenezo. Iwo sangathe kuchita kalikonse. "Iwo ndi ana a kusamvera."

"Anapatsidwa zosocheretsa zamphamvu, kuti akakhulupirire bodza, ndipo nkudzawonongedwa nalo ilo."

72 Zindikirani pamene dziko la mpingo silimamulandira Yesu, Mawu, owonetseredwa a tsiku limenelo, chifukwa (chiyani?) iwo anali nawo atawanthauzira Iwo mwanjira ina. Koma iwo bwenzi atadziwa kuti Iye anali Mawu amenewo, chifukwa chirichonse chimene Mulungu ananena kuti Iye akanadzachita, Iye anachichita. Ndipo Iye anati kwa iwo, "Fufuzani Malemba a ora lino; ndipo ngati ine sindikufikira pa muyezo umene unalankhulidwa kuti Ine ndidzachita, ndiye musandikhulupirire Ine."

Iwo anati, "Ife tikumukhulupirira Mose."

73 Iye anati, "Ngati inu mukanamukhulupirira Mose, inu mukadandikhulupirira Ine, pakuti Mose analankhula za Ine." Ndipo komabe iwo sanaziwone izo. Mulungu amene wa Kumwamba akufa pa mtanda, ndipo nkumanena mawu omwewo amene mneneri anati Iye akanadzanena, ndipo komabe iwo sanaziwone izo. Mukuona?

Iwo sanali a mtundu Wake. Iwo sanali Mawu, sanali Mawu ayi; ndipo iwo, komabe, iwo anali—anali achipembedzo kwambiri. Koma iwo sanali Mawu ayi, pakuti Iwo—Iwo akanazindikira malo Ake a ora limenelo.

74 Taonani momwe Malemba akulumikizirana limodzi mokongola mu m'badwo uliwonse. Zindikirani tsopano.

Ndipo pamene dziko la mpingo linakana kuti Mawu a Mulungu aziwalamulira iwo, iwo anamuvomereza wakupha, Barabasi. Kodi ichi chinachita chiyani? Icho chinamukweza Satana, mulungu wa m'badwo woipa uno, kufika pa malo amene nthawizonse iye anakhala akuwafuna.

Tsopano mvetserani. Pakuti, Satana sakulankhulidwa ngati mulungu wa m'badwo wina uliwonse koma m'badwo uno. Iye sanalankhulidwe kuti ndi mulungu wa m'badwo wa Nowa. Iye sanalankhulidwe kuti—kuti ndi mulungu wa m'badwo wa Mose, mulungu wa m'badwo wa Eliya. Koma, m'badwo woipa uno, iye ali . . . O, musaphonye izi! Iyeyo ndi mulungu wa m'badwo woipa uno, akupembedzedwa ndi mamilioni ndi mabilioni a anthu, ndipo iwo sakudziwa izo. Koma tiyeni tilole Lemba kuti limuyalutse iye mmawa uno, ndipo tiyeni tiwone, ndiye inu mudziwa. Mulole Lemba . . .

75 Monga mu misonkhano ya kuzindikira za mumtima, pamene Mzimu Woyera ufika pakati pa Mawu Ake ndipo Iye nkumutchula munthu uyu ndi kuti, "Iwe ulibe ntchito yakuti uzigona ndi mkazi wina uyu. Kodi iwe unachitiranji zimenezo, zaka khumi zapitazo, pamene iwe unkayenda ndi mkazi wa mwamuna uyo?" Kodi Iye akuchita chiyani? Kumuvundukula iye, kumuyalutsa Satana, yemwe wamumanga mwamunayo,

kapena mkazi wogona ndi mwamuna wa mkazi wina, kapena machimo amene iwo achita, zinthu zimene iwo achita. Kodi izo zimachita chiyani? Zimamuyalutsa iye.

76 Madokotala amatenga zipangizo ndipo amayesera kuti apeze chimene chavuta. Iwo sangathe kuchita zimenezo. Ife sitingathe kudziwa. Komano Mzimu Woyera umatulukira ndipo umadzaulula chimene iye ali, ndi kumuyalutsa iye. Mukuona? Ndicho chimene Mawu a Mulungu ali. Iwo ali Kuwala kumene kumawalira mu mdima.

Ndipo pamene iwe umva phokoso mchipinda, ilo nkumamveka mwachirendo; gulu la chinachake likugwira ntchito, ndipo iwe osadziwa kuti izo ndi chiyani. Uyatse nyali, msanga . . . Akajosolo, mphevu, izo—izo ndi ana a mdima. Ndipo pamene nyali yawala, izo zimabalalika.

"Iwo anachoka pakati pathu chifukwa iwo sanali a ife," Baibulo linatero. Mukuona? Iwo sangathe kukhala mu Kuwala kwa mdziko . . . Pakuti, Mulungu wa Kumwamba watumiza Kuwala Kwake mu masiku otsiriza ano, kuti Iye akathe kuwunikira njira ya ana Ake, kuti iwo asakayende mu mdima ndipo nkupunthwamo, koma kuti iwo akayende mu Kuwala kwa kunyezimira kwa Yesu Khristu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ameni!

77 Zindikirani, Satana samatchedwa mulungu wa m'badwo wina uliwonse koma m'badwo uno. Icho chinali chokhumba chake kuti adzakhale wofanana ndi Mulungu, kuyambira pachiyambi pomwe.

Tiyeni tiwerenge zimenezo. Ife tingotenga nthawi yathu. Tiyeni tibwerere mmbuyo ku . . . Onani, ine ndazilemba izo, Yesaya 14. Tiyeni tibwerere mmbuyo apa ku Yesaya 14, miniti chabe, ndipo tikawone zimene Mulungu ananena. "Mulungu," chimene Satana anachita. Yesaya 14:12 ndi 14. Zindikirani.

> *Wagwadi kuchokera kumwamba, O Lusifara, mwana wa m'banda kucha! wagwetsedwa pansi iwe, wolefula mafuko!*
>
> *Pakuti iwe unati mumtima mwako, ndidzakwera kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wachifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu* (ana a Mulungu, tsopano): ndipo *ndidzakhala pamwamba pa phiri la khamu, mmalekezero a kumpoto;*

78 Chinali chokhumba cha Satana kuti azipembedzedwa ngati Mulungu. Iye anatenga magawo awiri a atatu, magawo awiri a atatu a nyenyezi za Kumwamba. Anadzikweza yekha pamwamba pa nyenyezi zimenezo, ndipo analalikira kwa izo, ndipo ananyenga magawo awiri a atatu a iwo. Inu mukuona zimenezo? Chabwino. Zindikirani, ndicho chokhumba chake.

Ndipo tsopano iye wakonzeka, ndi mkwatibwi wake wosankhidwa mosamalitsa, wophunzira ndi chidziwitso chake chomwe, mwaona, yense wopentedwa mu chinyengo chake, cha nyumba zazikulu ndi zipembedzo zazikulu, ndi mapenti a chidziwitso ndi zaumulungu, ndi nzeru ndi luntha, ndi kuphunzira, kuti akanyenge dziko lonse, ndi kudzakhala "mulungu." Ndizo zimene iye wachita. Zonsezo zikudzathera mwa munthu wotsutsakhristu, yemwe wavekedwa kale nduwira "wolowa mmalo mwa Mulungu," ndi mkwatibwi wake wokonda mwachidziko, wa sayansi, yemwe wavekedwa nkuzikuza kwa luntha, maphunziro achipembedzo. Iye wapangidwa kukhala wachipembedzo mofanana ndi iye, ndi kutanthauzira kwake kwake kwa Mawu a Mulungu monga anachitira Eva, ndi monga mwana wake Kaini anachitira.

Tsopano inu munati, "Mwana wa satana?"

79 Mundisonyeze ine malo amodzi mu Baibulo pamene Kaini anayamba watchedwapo mwana wa Adamu. Baibulo linati iye anali "mwana wa woipayo," mbewu ya serpenti. Ayi, chophimbacho chachotsedwapo tsopano, m'bale. Piramidi yatsegulidwa, monga vumbulutso lawonetsera.

80 Zindikirani zimene iye adzachite, malingaliro ake. Iye ankaganiza kuti Mulungu amakhala mu kukongola kwa chidziko. Iye anachita zimenezo Kumwamba. Tchimo silinayambire nkomwe mmunda wa Edeni; ilo linayambira Kumwamba, pamene Lusifara, mwana wa mmawa, anadzikweza yekha mu kukongola, ndipo ankafuna ufumu wokongola kwambiri kuposa uwo wa Mikaeli. Ndipo iye ankaganiza kuti Mulungu amakhala mu kukongola.

81 Ndipo zindikirani Kaini. Iye sanafune nsembe ya magazi. Iye anatsika ndipo anapereka nsembe chipatso, kapena—kapena minda ya kukongola pa guwa lake. Wachipembedzo kwambiri, anachita chirichonse, chimene, chimodzimodzi basi monga Abele anachitira; anapereka nsembe, anagwa pansi pamaso pa Mulungu mu kupembedza, womvera mwanjira iliyonse, koma wopanda vumbulutso la Mawu.

Ndipo Mawu anali, kuyambira pachiyambi, dongosolo la Mulungu. Koma Mulungu anawulula, mwa vumbulutso, chinthu kumene chimene Iye anachitsimikizira ndipo anavomereza kuti izo zinali zolondola. Osati chipembedzo, osati guwa, osati kukhala wa mpingo, osati kupanga nsembe, osati kukhala wodzipereka; koma mwa vumbulutso la Mawu a Mulungu. Mulungu kuwulula kwa iye chimene icho . . .

Amayi ake sanadye apulo amene njoka inamupatsa iye, koma iye anagonana ndi munthu wa Satana, wamawonekedwe a chinyama; osati chokwawa, koma chophunzira kwambiri, chochenjeretsa cha mmunda monse, chifanizo cha munthu, chinthu chokhacho chimene mbewu ingasakanizikemo. Tsopano

sayansi ikuyesetsa kuti imupeze iye. Ndipo iwo sadzampeza konse iye, chifukwa fupa lirilonse mu thupi lake linasinthidwa. Koma Baibulo limanena kuti ziri chomwecho.

82 Zindikirani zimene munthu uyu ati adzachite tsopano. Munthu uyu, "Iye azidzakhala mu kachisi wa Mulungu," mmenemo ndi, mtchalitchi, "kumadziulula yekha kuti ndi Mulungu." Tsopano ngati inu mukufuna kuti muwerenge zimenezo, zimenezo ndi Atesalonika Wachiwiri 2:3 ndi 4, ndi Chivumbulutso 13:4, 11 ndi 12; pamene akulankhula, aneneri awiri onse, onse awiri Yohane ndi Paulo, cha chimene iye ati adzakhale mu masiku otsiriza. Tsopano inu mukawerenge zimenezo, chifukwa ine ndazilemba apa. Koma ine . . . kuti tisunge nthawi tsopano.

83 Tsiku limene ife tiri nkukhalamo limatchedwa, mu Baibulo, "tsiku la munthu," tsiku la munthu. Lino si tsiku la Mulungu. Mulungu si mulungu wa dziko lino; Baibulo limati Iye siali. Iye ndi Mulungu wa Kumwamba. Koma lino si tsiku la Mulungu.

Lero ndi tsiku losankha. Mwina, mukhalire moyo lero, ndi kufa; musankhe Mulungu, ndi kukhala moyo. Ndipo Mulungu ndi Mawu, ndipo Mawu ndi Mawu owonetseredwera ora ndi tsiku.

84 Zindikirani, "tsiku la munthu." Ngati inu mukufuna kuti mulembe zimenezo, ine ndinali woti ndiwerenga izo. Koma Akorinto Woyamba 5:1-5 . . . Akorinto Woyamba 4:1-5, mundikhulukire ine, Akorinto Woyamba 4:1 ndi 5, anali Paulo akulankhula za kuweruzidwa ndi munthu, mu tsiku la munthu.

85 "Tsiku, mumalitchuliranji ilo kuti ndi tsiku la munthu?" inu mungatero. Ilo ndi tsiku limene zintchito za chidziwitso cha munthu zikukuzidwa.

Taonani chimene, kubwekerera konseku kwa chikominisi, winawake kuyesetsa kuti amutengere wina apite ku mwezi. Mulungu akuyesetsa kuti amutengere wina apite Kumwamba. Mukuona? Koma taonani momwe iwo akuwonongera mamilioni ndi mabilioni ndi matrililioni a madola, mu kuyesetsa kopanda phindu. Pamene iwo ati akafike uko, iwo sakapezako kanthu kalikonse. Vuto ndi chiyani ndi iwowo?

Ine sindikusamala za mwezi. Ine ndikufuna ndidzawudutse mwezi mwaliwiro kwambiri ine sindidzawuwona nkomwe iwo; kumangopitabe mmwamba. Ine ndikufuna ndidzadutse Milky White Way, kumapitabe, kumakhala ndikupitabe. Inde!

86 Ndipo dziko lero likudzipereka lokha kwa chidziwitso chimene chinabwera ndi Satana. Ndipo tsiku la munthu likulemekezedwa, osati ndi Mawu a Mulungu, koma ndi chidziwitso chimene iye ali nacho.

Tsopano taganizani. Mulole izo zilowerere mkati. Ndipo pamene inu muzikaseweranso tepi iyi, pa mfundo iyi apa, mudzaime kwa kanthawi ndipo mudzaganizire.

Ntchito zake zikukwezedwa kuposa Mawu a Mulungu ndi ntchito zowonetseredwa; nzeru ya Satana, imene iye anampatsa Eva pachiyambi. Tsopano tamvetserani; musaphonye izi. Nzeru za Satana zakwezedwa mpaka pa mpando wachifumu wa kupembedza, mwa munthu, kuposa Mawu a Mulungu otsimikiziridwa a orali. Mipingo yathu ikutsimikizira zimenezo mwa maseminare—awo, masukulu a kuphunzira, amene aphunzira kuposa momwe Mawu a Mulungu amadziwira za Izo, iwo akuganiza. Ndipo uko, Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti*, ndipo Mphunzitsi *Wakuti-ndi-wakuti*, ndi Purofesa *Wakuti-ndi-wakuti* akweza chidziwitso chawo chomwe, chotchedwa (kuchokera kwa Satana) choonadi, kuposa lonjezo lotsimikiziridwa la Mulungu, likupangidwa kumveka pamaso pawo pomwe. Ndipo munthu akugwera zimenezo. Mukuona?

87 Zopindula zake za sayansi, kuyesera kutsimikiza kuti Mawu a Mulungu ndi olakwika. Tangoganizani za zimenezo. Iye, zake, zimenezo ndi, maganizo a munthu, kufotokoza Mawu a Mulungu kwa anthu, ndi kuwapanga Iwo kukhala opanda mphamvu kachiwiri, monga iye anakhalira nazo izo mu m'badwo wa chipembedzo pamene Yesu anawonekera pa dziko lapansi. Yesu anati, "Inu achinyengo! Inu, ndi mwambo wanu," kumeneko ndi kutanthauzira kwawo, "awatenga Mawu a Mulungu ndi kuwapanga Iwo kukhala opanda mphamvu kwa anthu." Ndipo ndicho chinthu chomwecho chimene iwo achita lero. Iwo alibe mphamvu.

88 Zindikirani, "Iwo," anthu, "amukweza iye pamwamba pa zonse zotchedwa Mulungu." Kodi Atesalonika Wachiwiri samanena kuti iwo akanadzachita zimenezo? Ndipo ulamuliro wa mpingo wa chipembedzo, anthu kumakhulupirira chipembedzo chimenecho kuposa momwe iwo amamukhulupirira Mulungu. Ndipo Mulungu ndi Mawu. Iwo amakhulupirira kachikhulupiriro ka chipembedzo chawo kuposa Mawu, kamene "kamamukweza iye kuposa zonse zimene zimatchedwa Mulungu." Ndipo alipo Mulungu mmodzi yekha, ndipo ameneyo ndi Mawu.

"Zonse zotchedwa Mulungu; kotero iye monga Mulungu akukhala mu mpingo wa Mulungu, kumatsimikizira kuti iye ndi Mulungu," chifukwa iye ali nawo anthu akumupembedza iye. Mulungu ndi Mawu. Ndipo iye akudzikweza yekha pamwamba pa zonse zotchedwa Mulungu. Ndipo alipo Mulungu mmodzi yekha, ndipo Mulungu ameneyo ndi Mawu. Mukuona? "Ndipo zonse zotchedwa Mulungu," ali, mulungu wa m'badwo uno wadzikweza yekha pamwamba pa Mawu owona, otsimikiziridwa a Mulungu. Ameneyo ndi Yohane Woyera 1. Mukuona? "Pamwamba pa zonse zotchedwa Mulungu, kotero

kuti iye ngati Mulungu akukhala mu kachisi wa Mulungu," ndi ulamuliro.

Taonani, ndipo iye akutamandidwa chifukwa cha izo! O, muwalole anthu, Mulungu, awone chinyengo chimenecho! Iye akutamandidwa chifukwa cha zimenezo, ndipo mwaulemu kumakhulupiririridwa ndi anthu a m'badwo woipa uno. Tsopano kodi inu mukumuwona mulungu ndi antchito ake a m'badwo woipa uno?

89 Tsopano tiyeni tiziwone izo zikuwonetseredwa. Iye akuti iye akupanga dziko labwinoko kuti iwo azikhalamo, mwa chidziwitso chake pambali pa Mawu a Mulungu osalephera. Koma pakubwera kwake limodzi, mu zipembedzo, ndi tizikhulupiriro, ndi luntha, ndi mwasayansi, ndi zina zotero, iye akupanga dziko labwinoko kwa munthu kuti azikhalamo, ndipo nkumanyalanyaza lonjezo la Mulungu, kuti nthawi yokhayo imene dziko liti lidzakhale loyenera kukhalamo ndi mu Zakachikwi. Inu mukudziwa, kuganiza kwanga, iye wapanga dziko labwinoko kuti azichimwiramo mmalo moti azikhalamo.

90 Zindikirani. Kodi iye anachita zimenezo? Iye waloleza tchimo. Iye waloleza kumwa kwa mowa, kusuta kwa ndudu. Ndipo mu matchalitchi, waloleza kuti mkazi akhoza kukhala membala wa mpingo, ali ndi tsitsi lalifupi. Tsopano kodi inu mungaime miniti imodzi yokha.

91 Mkaziyo akhoza kuvala akabudula, kuzipentapenta, ndipo nkukhalabe wa gulu lake la chipembedzo, zimene mwamtheradi ndi zotsutsana ndi Mawu a Mulungu. Iye amati ziri bwino. Mukuona chidziwitso chake? "Kodi zimenezo ziri ndi chochita chanji ndi mkazi?" Chimodzimodzi basi monga kudya chipatso choletsedwa, kapena osati chipatso choletsedwa, ndicho chimene icho chiri. Mulungu anati asachite izo, koma iye amachita zimenezo.

92 Ndipo iye amamukhulupirira iye, ndipo iye amamukonda iye chifukwa cha izo. Mkaziyo amadana naye Mulungu. Zochita zake zomwe zimatsimikizira kuti iye amatero. Mkaziyo amanena kuti amamukonda Iye, koma iye amamukonda Satana. Iye amamupembedza mulungu wa fashoni, mulungu wa mdziko, mulungu wachikazi wa Hollywood. Iye amamukonda iye, koma iye amadana nawo Mawu owona a Mulungu, amene ali Mulungu woona yekhayo amene alipo.

Akuloleza izo mmatchalitchi. "Palibe chovuta. Akazi athu akhoza kuchita *izi*, *izo*, kapena *zinazo*." Koma Pamaso pa Mulungu wamoyo, iye samalolezedwa ngakhale kuti abwere, pokhapokhapo ngati akulapa.

93 Akuziwona, kuti iye ndi mulungu wa kukongola kwa chidziko, iye ali. Mkaziyo amafuna kuti aziwoneka wokongola. Ndipo mkaziyo ndi mulungu wa kukongola, kuyambira pachiyambi. Iye akhoza, ndipo wakwanitsa mwa chidziwitso

chake mu sayansi ndi zinthu zogwirika, kuti amukonzere kukongola wake, m'badwo wachitsanzo uno...m'badwo wamakono uno, kani, woipa. Iwo wapangidwa mokongola.

94 Zindikirani. Izo ndi zofunika kuzizindikira. Pachiyambi, Seti ndi ana ake sanapite konse njira ya mwasayansi.

Tsopano ife tilankhula za sayansi kwa maminiti pang'ono. Ngati ine ndinganene izi, sindikupepesa chifukwa cha umbuli wanga; koma, gulu la mbuli, chirichonse chimene chingawakane Mawu a Mulungu. Mukuona? Zedidi.

Ndi zofunika. Penyani izo. Ana a Seti sanapite njira ya mwasayansi. Iwo anali azibusa odzichepetsa, alimi, ndi zina zotero.

Koma ana a Kaini anatero. Bwanji? Anadzozedwa ndi adadi awo, mdierekezi. Kaini, anadzozedwa ndi adadi ake, mdierekezi, ndi awa amene anadzozedwa ndi mbewu imeneyo kumatsika mmusi.

95 Penyani mbewu ya Mulungu ikutsika mmusi kudutsa m'badwo uliwonse, ndipo muwone kumene izo zikulunjika lero. Akhristu, Akhristu enieni, onsewo si a kafukufuku wa sayansi ndi zinthu. Ayi. Miniti chabe, ife tilowa mu zimenezo.

Koma Kaini ankatero, motsatira khalidwe la bambo awo, mdierekezi, wodzadza ndi chidziwitso cha chidziko, kukongola, ndi sayansi, zina zotero. Ana a Kaini anali a sayansi. Iwo anali ophunzira. Iwo anali oyimba nyimbo—zing'wenyeng'wenye za nyimbo; Elvis Presley wamakono, zina za zinthu izi zonga zimene bodi ya sukulu imazilola kuti zizichitika kuno mu msewu usiku wa Loweruka lirilonse. Omanga mzinda, kuwakongoletsa akazi kwa chisiliro chawo, ngati mdierekezi kuwapatsa akazi penti, ndi kumadula tsitsi lawo, ndi kuwaika iwo mmakabudula, ndi zinthu monga choncho. Iwo, izo ndi za kwa chisiliro chake chauve. Uko ndi kupanda psyete, koma ine sindikudziwa njira ina iliyonse yomwe ndinganenere izo.

96 Tsopano, ife tikudziwa kuti uthenga wa Satana ndi uthenga wa sayansi ndi kutukuka. Iye anawulalikira iwo mu Edeni; osati Mulungu; Satana anatero, sayansi ya kutukuka. Sayansi ndi kutukuka ndizo uthenga wa Satana. Muwone kumene iye watitsogolera ife lero, ndi izo. Mukuona?

97 Zindikirani, iye anawulalikira iwo mu Edeni, kwa ndani? Kwa mkwatibwi wa Adamu. Ndipo iye anagwera iwo. Iye anamunyenga iye kuti akakaikire amodzi a Mawu a Mulungu. Tiyeni tiwone zimene iye ayenera kuti ananena. Iye ayenera kuti anati, "Siziri mwa sayansi kuti ungafe, mu mpingo woyera uno." Kapena, "Inu muikidwa pa sukulu ndi kuphunzitsidwa, kuti musamakhulupirire zinthu zopandapake zoterozo monga imfa. Ine sindikusamala ngati Mawu a Mulungu ananena izo; izo nzopandapake."

98 O, tamuonani iye lero. “Mulungu ndi Mulungu wabwino. Inu muli mu mpingo Wake woyera; bwanji, inu simungafe.” Koma Mulungu anati inu mudzatero, ndipo izo zikukhazikitsa izo. Mukumuwona iye lero? “O, mungokhala wa tchalitchi. Sizimatengera zimene iwe ukuchita, kapena *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*. Mungobwera ku tchalitchi ndipo mudzangokhala membala wabwino. Kumadula tsitsi lanu, ndi zamkhutu. Ndi kumavala akabudula, ndi kumadzipentapenta, ndi kumapita kukavina, ndi mowa pang’ono apo ndi apo, sizingakupwetekeni inu, bola ngati inu simukulowelera mu zimenezo. Kunena moona, ine ndikukhumba ana inu mukanamwapo, kuti iwo akathe kuphunzira ngati iwo angazikonde izo kapena ayi.” Ndi ameneyotu, mulungu wa m’badwo uno, m’badwo woipa uno.

99 “Mulungu ndi Mulungu wabwino.” Ine ndamvapo zimenezo mochuluka kwambiri mpaka ine ndimadwala. Mulungu nayenso ndi Mulungu wa chirungamo. Iye si agogo okalamba amisala amene angamakankhidwekankhidwe, ndipo zidzukulu Zake ziribe tchimo lirilonse. Iyeyo ndi Mulungu wa chirungamo ndi wa chiyero. Iye anazitsimikizira izo mmunda wa Edeni, mwa ana Ake oyamba. Inu mukawoloka mzere umenewo, wa amodzi a Mawu Ake, inu mwafa. Chinthu chomwecho chiri lero.

100 Ndipo zindikirani, iye analalikira uthenga wa mtundu umenewo wa sayansi, wa chisangalalo, wophunzira, wa chitukuko kwa Eva, ndipo mkwatibwi wa Adamu anakhulupirira izo. Ndipo iye wapambana pomuzadza wotchedwa mkwatibwi wa Khristu, mpingo wa Adamu Wachiwiri, ndi mtsutsano womwewo. Uko nkulondola.

101 “O, izo si—izo si za Mulungu; Mulungu ndi wabwino kwambiri kuti angachite zimenezo. Bwanji, bola ngati inu mumapita ku tchalitchi. ‘Ngati inu mukukhulupirira.’” Mdierekezi amakhulupirira; osati kudzipangitsa kukhulupirira, koma iye amakhulupirira kwenikweni. Iye sanapulumutsidwe. “‘Ngati inu mukhulupirira.’” Huh!

102 Iye akumuuza mkwatibwi wachiwiri, kapena Mkwatibwi Wachiwiri wa Adamu, chimodzimodzi monga iye anamuuzira woyamba. Monga ngati, “Tsopano, machiritso Auzimu, kulibeko chinthu choterocho. Ife tikhoza kutsimikizira zimenezo. Sipanayambe zatsimikiziridwa kuti zinachitikapo.” “Ndipo ubatizo uwu mu Dzina la Yesu, tsopano kodi inu simukuzindikira kuti ndine ulamuliro wa mpingo?” iye akuti. “Ife tinagwirizana zimenezo ku Nicaea, Roma,” pamene mizimu itatu yakuda iyo inatuluka kuchokera mwa chinjoka, aneneri abodza, ndi zina zotero. “Ife timakhulupirira kuti ulipo utatu wa Amulungu.” O, kalanga ine! Zimenezo ndi chikunja basi monga zingakhalire. Inu musadzabwere konse kwa Mulungu ndi chinthu ngati chimenecho, kudzayesera kudzaima Pamaso Pake. “O, izo sizipanga kusiyana kulikonse ngati inu mubatizidwa mu

maudindo a 'Atate, Mwana, Mzimu Woyera.' Kodi izo zimapanga kusiyana kotani?"

103 Izo zinapanga kusiyana kochuluka kwambiri, mpaka Paulo analamulira gulu la Abaptisti kuti iwo amayenera kuti abatizidwenso mu Dzina la Yesu Khristu Mzimu Woyera usanabwere konse pa iwo. Ndipo zinampangitsanso mtumwi uja kuti akuwe, ndi kuti, "Ngati mngelo abwera kuchokera Kumwamba ndipo nadzalalikira china chirichonse, iye akhale wotembereredwa." Zedidi, izo zimapanga kusiyanitsa. O, mai!

104 "Kulibeko chinthu chotero monga ubatizo wa Mzimu Woyera mmasiku ano. Zimenezo zinali za ophunzira okha. Izo zinatha. Ndi chinthu chotero monga aneneri? Izo sizimadziwika nkomwe. Zozizwitsa? Izo si za mwasayansi. Malaki 4? Zimenezo zinali za m'badwo wina. Yohane 14:12? O, Yesu samatanthauza kwenikweni zimenezo. Luka 17:30? O, zimenezo zinali nthano chabe. Mwaona, izo—zinatanthauziridwa molakwika; izo sizinali pachiyambi." Zovunda zoterozo!

Pamene Mulungu Wamphamvuzonse amabwera pakati pathu ndi kudzatsimikizira izo. Pamene Iye amanena, kuti, "Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," Iye amatsimikizira izo chomwecho. Ine sindikusamala yemwe amatsutsa za izo; Mulungu amatanthauzira Mawu Ake Omwe. Iye anati Iye akanadzachita chinthu ichi mu masiku otsiriza. "Padzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo." Ndipo Kuwalako kulipo, kwa kuwonetseredwa kwa Mwana wa Mulungu.

105 Dzuwa lomwelo limene limatulukira kummawa ndi dzuwa lomwelo limene limakalowa kumadzulo. Mneneri anati, "Lidzakhalapo tsiku limene silimadzatchedwa masana kapena usiku." Ilo ndi lachimbuuzi, mitambo, itaphimba nkhope ya dzuwa. Koma anati, "Mu nthawi ya kumadzulo padzabwera Kuwala kachiwiri." Mwana yemweyo! Iye ali Alpha ndi Omega. Mwana yemweyo yemwe anatulukira kummawa ananenedweratu kuti adzakatulukira kumadzulo kachiwiri, mu masiku otsiriza, basi tsikulo lisanathe. Ine sindikudziwa mmene iwo amatanthauzira Izo; Mulungu amatanthauzira Mawu Ake Omwe. Iye amawatsimikizira Iwo. Ino ndi nthawi ya kumadzulo.

106 Ndi zachisoni, koma ndithudi iye anagwera zimenezo kachiwiri. Mkwatibwi wa Khristu anagwera izo, ndipo anatenga chidziwitso cha luntha la mlaliki wina waku seminare mmalo mokhulupirira Mawu a Mulungu angwiro, otsimikiziridwa.

107 Tsopano atumiki kunja uko mu dziko kulikonse kumene inu muli, inu mukhoza kusagwirizana nacho Ichi. Ine sindikukupwetekani inu. Ine basi ndikungoyesera-. . . Ine ndikulankhula kwa gulu langa lomwe. Ine ndikungoyesera . . . Ngati inu mukufuna kuti mukhazikike, ine ndithudi ndikhala wokondwera kuti mumvere Izi. Ndiyeno mumvetsere pa Izi.

Mukuona? Koma ine ndikungowauza iwo chimene iwo ali nacho—zimene iwo aziwona, ndi kusonyezera izo kwa iwo; Mulungu kutsimikizira izo, kuti izo ndi zoona. Mukuona?

Ora lake ndi lino. Sizikusowa aliyense kuti atanthauzire Izo. Chidziwitso chanu cha chidziko chiribe chirichonse... Inu mukhoza kukhala ndi B.A., D.D., A.D., kapena chirichonse chimene chingakhale; icho sichikutanthauza chinthu chimodzi. Mulungu amatanthauzira Mawu Ake, Iyemwini. Iye analonjeza izo, ndipo ndi izi apa.

108 Koma mwa chidziwitso cha ku seminare, kulalikira kwa chipembedzo, "kwapangitsa dziko lonse kuti lizizizwa nacho chirombo chimene bala lake la ku imfa linachiritsidwa," kuchokera ku chikunja kupita ku upapa. Kodi mukuona kumene akulunjika? Iye akukhulupirira izo. Iye akukhulupirira chidziwitso chimene iye amamuuza.

109 Izo ziri, tsopano penyani, ndi zakuti akwatibwi otomeredwa onsewo akhulupirira chidziwitso cha Satana motsutsana ndi Mawu a Mulungu. Mkwatibwi wa Adamu anakhulupirira chidziwitso cha Satana motsutsana ndi Mawu a Mulungu, ndipo mkwatibwi wa Khristu wakhulupirira chidziwitso cha Satana, mu m'badwo waluntha uno, motsutsana ndi Mawu a Mulungu.

Ndipo zindikirani. Eva, mwa chirengedwe, amene anakhulupirira izo, ndipo anawugwetsera mtundu wonse wa anthu mu imfa. Mkwatibwi wachirengedwe! Adamu, munthu wachirengedwe wa padziko lapansi; mkwatibwi wake, mwamunayo asanafike kwa iye, kuti akhale mkazake, anawugwetsera mtundu wonse wa anthu mu imfa. Kaya ndi mwasayansi kapena ayi, ife tikufa chimodzimodzi basi, chifukwa Mulungu anati ife tidzatero.

Kaya inu muli mu Edeni woyera, kapena mpingo woyera, kapena chipembedzo choyera, kapena chirichonse chimene chingakhale, inu mudzafa tsiku limene mudzakaikire Mawu amodzi a Mawu a Mulungu kuti ali Choonadi, pamene Iwo avomerezedwa ndi kutsimikiziridwa kwa inu. Ndiro tsiku limene inu mudzadzilekanitse nokha ndi Mulungu. Osati kokha chiganizo chonsecho; Mawu amodzi. "Aliyense amene adzawonjezera mawu amodzi, kapena kuchotserapo Amodzi," ndiro tsiku limene inu muti mudzafe.

110 Zindikirani, mkwatibwi wa Adamu anayambitsa imfa yachirengedwe kwa mtundu wake, mtundu wa anthu.

Ndipo mkwatibwi wa Adamu Wachiwiri, mkwatibwi wotomeredwa ndi Khristu, wawugwetsera mpingo wonse kupita mu imfa yachipembedzo, kuti ukatenge chilemba cha chirombo, mwa zipembedzo zazikulu, zasayansi, zaluntha. "Ndife a Baptisti. Ndife a Presbateria. Ndife a Pentekoste," ndi zina zotero. "Ife tiri ndi *izi*, ndipo ife tiri ndi katundu wambiri. Ife, ife timadziwidwa ndi boma. Ife tiri konsekonse mdziko," ndi zinthu

zonse zoterozo. "Ndipo opambana, ndi a meya a mzinda, ndi ena otero, amabwera kwa ife. Ngakhale a Purezidenti amabwera kudzakhala pa misa ndi ife, ndipo amabwera kwa *izi*, *izo*, kapena *zinazo*." Dziko lonse laponyedwera ku imfa yauzimu, yachipembedzo; mpingo wonse. Iye wafa!

Inu mukuti, "Inu mukutenga dera lalikulu."

111 Yesu anati, "Monga izo zinali mu masiku a Nowa, mmene miyoyo eyiti inapulumutsidwa, chomwechonso zidzakhala pakudza kwa Mwana wa munthu." "Mu masiku a Loti, mmene atatu anatulutsidwa kuchokera mu Sodomu, pa tsiku limenelo . . ." Tsopano liripo kale gulu limene latuluka kale, kumbukirani. "Koma, monga zinali pa nthawi imeneyo, pamene Mwana wa munthu ati azidzawonetseredwa." Taonani tsiku lakelo, taonani pamene ife tiri!

112 Tsopano iye wapangitsa dziko lonse kuti livomereze ulamuliro wa sayansi wa madongosolo a maphunziro amene Satana wawapereka kwa iye pansi pa dzina la tchalitchi, utsogoleri wa dongosolo la maphunziro, a sayansi. Ine ndikujambula kwa inu mulungu wa dziko lino.

Pamene iye, monga Eva, anali ndi kudzadza kumene kwa Mawu a Mulungu mdzanja lake, iye akanakhoza kutenga Mawu a Mulungu. Koma kodi iye anachita chiyani kwa Iwo? Mmalo moti adikirire ubatizo wa Mzimu Woyera, analola kuti sayansi itsimikizire kwa iye kuti Mzimu Woyera unali kokha wa ophunzira.

Mmalo moti asiye machiritso Auzimu kuti azipitirira, pamene tsopano iye amayenera kuti azidzutsa akufa ndi kumachita zozizwitsa zazikulu; iye wamuloleza Satana, pansi pa utsogoleri wake wa munthu wachipembedzo, kuti atenge Mawu a Mulungu ndi kuyesera kumanena kuti Iwo anali a m'badwo wina. Ndipo iye wakhulupirira zimenezo.

113 Pamene, Baibulo linati, "Zinthu zimene ine ndikuzichita inunso muzidzazichita." Yesu ananena zimenezo. "Pitani inu ku dziko lonse ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse." Ife tikadalibe zolengedwa. "Zizindikiro izi zidzamutsata aliyense wa iwo amene akukhulupirira." Iye amakana chidutswa chirichonse cha Iwo.

114 Iye amakana zauzimu zonse, ndipo iye anasinthanitsa Iwo ndi kumvetsa kwake kwaluntha kwa Baibulo; kumene ansembe, ndi bambo woyera, otchedwa chomwecho, kumene mabishopu, alikibishopu, kumene oyang'anira boma, apenyi, ndi zina zotero, aikamo kutanthauzira kwawo kwawo kwa Iwo. Ndipo Mulungu wawasiya iwo, atakhala pamenepo, akufa ngati thwelofu koloko.

Zinthu zokhazo zimene zatsalira mu masiku otsiriza ndi gulu la Achipentekoste lapang'ono lokhala ndi mulu

wa nyimbo zophokosera zolimba mmene iwo angathere, kumathamanga thamanga pansipo, kumalankhula mmalirime ndi kumafuula, "ndi kumakhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Mawu ake." Kumawauza iwo kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu; kuseka pa nkhope yako. Koma, izo, Mulungu amapitirirabe kukazipanga izo kukhala chimodzimodzi basi, kutsimikizira Mawu Ake kuti ali chomwecho.

115 Zindikirani, mtengo umene Satana anamupangitsa Eva kuti adyeko, unali "mtengo wa chabwino ndi choipa." Iwo unali mtengo wosakanizikana.

Tsopano taonani tsiku limene ife tiri nkukhalamo, pamene Iye ali kuitana atuluke Mkwatibwi. Iye ali nawo mpingo umene umadzinenera kuti ukuchita bwino, pamene iwo ndi woipa, pa kuwakana Mawu. Mtengo wosakanizikana. O, mukuti, "Iwo—iwo ali ndi magulu aakulu. Iwo—iwo—iwo—iwo amathandizira *izi*. Ndipo a Red Cross amavomereza izo. Ndi masukulu onse, iwo . . . Taonani apa!"

O, koma kungokana Mawu amodzi, ndicho chokha chimene inu muyenera kuti muchite kuti mufe; ziribe kanthu kuti ndi zaluntha bwanji, ndi zabwino bwanji. Yesu anati, "Chimera pang'ono chimatupitsa mtanda wonse." Malo amodzi a chimera amawononga mtandawo. Mawu amodzi a Mulungu, akaikidwa pamalo olakwika, amawononga Chithunzi chonsecho. Nanga bwanji nkono wanga ukakhala pamene phazi langa liyenera kukhalapo? Mukuona? Nanga bwanji ngati khutu langa litakhala pansi apa pamene dzanja langa liyenera kukhalapo? "Chimera pang'ono chimatupitsa mtanda wonse."

Mukuti, "Inu mukudziwa bwanji kuti Iwo ndi olondola?" Mulungu amawatsimikizira Iwo molondola. Iye amawatsimikizira Iwo. Iye ananena Izo apa mu Mawu, ndiye Iye amawatsimikizira Iwo. Ndi momwe ife timadziwira kuti Iwo akulondola kapena ayi.

Kungokana Mawu amodzi ndicho chonse chimene chimatengera kuti ufe. Iwo anabweretsa zotsatira zomwezo mu m'badwo woipa uno, imfa yauzimu, monga inachitira imfa yathupi kwa mtundu wonse wa anthu.

116 Taonani momwe Satana anawutengera m'badwo wa sayansi uwo kumbuyo uko, wa Nowa, kukatsamira pa kumvetsa kwawo kwawo. Huh! Baibulo limatiuza ife, mu Miyambo, "Musatsamire ayi pa kumvetsa kwanu kwanu." Ndipo, "Musiye mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo a Mulungu akhale owona." Koma Satana, mwa chidziwitso chake, kuyambira pachiyambi mmunda wa Edeni, anawapangitsa anthu kuti azitsamira pa kumvetsa kwawo kwawo. Ndipo, inu mukudziwa, kudzera mu ntchito zake zazikulu za Max Factor zimene iye anali nazo kumbuyo uko, anawapanga akazi kuti akhale okongola

kwambiri mwakuti izo zinapangitsa mwana wa munthu. . . ana aamuna a Mulungu, kani, kuti akagwe ndi tchimo ndi kuwakwatira iwo. Kulondola. Iye . . . Akazi anali owoneka bwino kwambiri, okongola kwambiri.

117 Tsopano inu mumutenge mkazi wamba pa msewu lero. Ambiri a inu munawerengapo nkhaniyo; inu simunayambe mwamvapo izo, asanafike masiku anga. Pearl O'Brien, ndi angati anayamba amvapo za iye? Zedi. Iye ankatchedwa mkazi wokongola kwambiri pa dziko lapansi. Bwanji, palibe mwana wa sukulu amene amapita ku nyumba ya sukulu lero koma yemwe ndi wokongola pawiri kuposa iye anali. Chifukwa chiyani ziri tero? Kukongola kwa akazi kuli koti kudzachitike mmasiku otsiriza.

Iwo adula tsitsi lawo. Iwo awaika iwo mu timadiresi tating'ono ta atsikana. Iwo avala akabudula, ndi mapanti, ndi zirizonse zimene inu mumadzitcha izo, pa iwo. Iwo amapaka penti, ndi zophoda zofiira, ndi mtundu wonse uwu wa zinthu, kuti awapange iwo chinachake chimene iwo siali. Mukuona? Koma podzera mu chidziwitso cha sayansi iwo akwanitsa kuti achite izi. Kodi inu mukudziwa kuti pakuperekedwa ndalama zambiri pa zodzola za akazi, kuposa zimene ziripo, mu United States, kawiri kapena kuchulukitsa katatu kuchuluka kwake, zimene amagulira chakudya kuti azidya? Tsimikizirani zimenezo, izo nzoona, pa zodzoladzola.

118 Zindikirani, "Ana a Mulungu anawona ana aakazi a anthu," osati ana aakazi a Mulungu, "ana aakazi a anthu, kuti iwo anali okongola," ndipo izo zinawapangitsa ana a Mulungu kuti agwere mu chosocheretsa ichi. "Ndipo anatenga akazi a mtundu umenewo ndipo anawakwatira iwo," ndipo izo zinabweretsa m'badwo wa chiwerewere, chimodzimodzi basi monga izo zili lero; monga izo zinali mu Sodomu, monga izo zinanenedweratu kuti zidzakhala lero.

Kuti, pamene amuna ndi aakazi a tsiku la lero akumasinthana akazi. Ngati iwo sakumufuna mkazi uyu, iwo—iwo apita ku Reno, Nevada, ndi kukakwatira; ndi, kapena kukamusudzula, ameneyo, ndi kukwatiranso mu maminiti fifitini. Ndipo akazi akongola kwambiri mwakuti iwo ndi osati ungaziletse. Ndipo ndi chiyani chimenecho? Mdierekezi! Satana akadali apabe mu kukongola? Zindikirani.

119 Zindikirani, tchimo limenelo silinakhulukidwe kwa iwo. M'badwo wokongola uja, wa sayansi unali m'badwo woyipa kumene umene Mulungu anawuwononga kuwuchotsa pa nkhope ya dziko lapansi; m'badwo wokongola uja, wa sayansi. Yesu anati izo zidzachitikanso kusanati kudza kwa Mwana wa munthu. Nkulondola uko? Zindikirani, Yesu anati, "Monga izo zinali mu masiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu," pamene iwo onse anayesera

kuti akwatire. . . Tsopano penyani, “Ana aamuna a Mulungu anakwatira ana aakazi okongola a anthu,” ndipo Mulungu sanawakhulululukire konse iwo chifukwa cha izo.

120 Chimodzimodzi basi ndi chiphunzitso cha Balaamu, kuti iye anawapangitsa akazi okongola, aluntha, a sayansi aku Moabu kuti. . . okhala ndi maso awo odolola, mapenti ake ndi mapaudala, mafuta ake abwino onunkhiritsa, kuti akawadolole ana aamuna a Mulungu; kuwasiya akazi awo omwe amagwira ntchito ndipo amakhala ndi zikang’a mmanja mwawo, opanda zozipakapaka. Anawadolola iwo, ndipo, “Tiyeni ife tikwatirane wina ndi mzake, chifukwa ife tonse ndife anthu amodzi.” Limenelo linali bodza! Ilo linali bodza—bodza, ndiponso chopindula cha mdierekezi, kuti akawapangitse ana aamuna a Mulungu akwatire—ana aakazi a anthu.

Ilo linali bodza la mdierekezi, kuti Balaamu, mneneri wabodza uja, kuti ayesere kunenera motsutsa Mose yemwe ankayetsetsa kugwira mtunduwo pamodzi; kumanena kuti, “Chabwino, ife tikukhulupirira Mulungu yemweyo. Ife timapereka nsembe zomwezo. Ife tiri ndi nsembe zomwezo. Ife timachita chirichonse mofanana basi.”

“Moyandikana kwambiri mwakuti izo zikananyenga Osankhidwa ngati kukanakhala kotheka.” Mukuona? [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Chokaniko kwa iye, anthunu! Inu mulibe kanthu kochita naye iye!

121 Zindikirani, izo sizinali zachidziwikireni kuti Mulungu akanatanthauzira Mawu Ake kwa kam’badwo koipa ka Kaini. Ayi. Mulungu sakanatanthauzira Mawu Ake kwa iwo. Zindikirani . . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

Mulungu, chidziwitso cholipanga dziko kuti likhale lokongola kwambiri ndi la sayansi ndi lochimwa, Iye ankayenera kuti aliwononge ilo? Kodi Mulungu akanachita zimenezo, kulipanga dziko lokongola kwambiri; taonani apa, Mulungu kuwapanga ana Ake aakazi okongola kwambiri, ndipo nkuwaveka iwo mwachigololo kwambiri, kuti ana Ake aamuna adziwasilira iwo ndipo nkuchita nawo chigololo? Chiyani? Mulungu angachite chinthu ngati chimenecho?

Gulu ili lamaliseche, lodzivula la ma Laodikaya, kumapembedza mulungu wa dziko lino, kudzera mu mbalume zawo, ndi maphunziro, ndi ukathyali, ndi kukongola! “Tulukani pakati pake,” Baibulo linati, “musakhale otenga nawo a machimo ake, ndipo musalandire miliri yake.” Mulungu adzavumbitsa matalala kuchokera mmilengalenga tsiku lina, aakulu ngati mapaundi handiredi amodzi, ndipo adzamuwononga iye pomugenda; monga Mawu Ake nthawizonse amanena kuti Iye anatero, malamulo Ake.

Chabwino, ngati Mulungu atachita chinthu ngati chimenecho, kuwulula Mawu Ake kwa anthu oterowo monga

iwo, Iye angakhale—akugonjetsa cholinga Chake Chomwe. Mulungu si wopusa. Iyeyo ali gwero la chidziwitso chonse.

Kotero inu mukuona kumene zinthu zimenezo zikuchokera? Izo zikuchokera kwa Satana, ndipo izo zikadali apabe za Satana. Ndipo mpingo wakhulupirira zimenezo.

122 Tsopano inu mukuona, akazi, ine ndikuyesera mwakukhoza kwanga kuti ndikusonyezeni inu Mawu a Mulungu. Baibulo linati, "Ngati mkazi adula tsitsi lake, iye amanyozetsa mutu wake," chimene chiri mwamuna wake. Ndipo mwamuna wake ndi mutu, limodzi ndi Mulungu, kotero iye amanyozetsa Mulungu ndi mwamuna wake.

123 Tsopano izi zikusonyeza yemwe ali mutu wa kachitidwe ka mpingo wa chidziko. Izo zikusonyeza yemwe ali mutu wa ilo. Ndi Satana, mmawonekedwe a munthu wapamwamba, munthu wa chidziwitso, chidziwitso chapamwamba. Iye amadziwa kuposa ena onse a iwo. Ziribe kanthu kuti Mawu akuti chiyani, iye—iye ali nako kutanthauzira kwake kwake kwa Iwo, mwaona, kutanthauzira kwa m'badwo woipa uno.

124 Zindikirani mapulani ake oti amange tchalitchi cha chipembedzo chapamwamba, Mipingo ya Dziko lonse Lapansi, mwaona, chipembedzo chapamwamba, ndicholinga chakuti dziko lonse lidzimupembedza iye, chirombo, pansi pa dzina la Chikhristu chimodzi. Kodi inu mungafune kuti muwerenge zimenezo mu Baibulo? Chivumbulutso 13:6 ndi 8. Iyo ndi nsanja yamakono ya Babulo.

125 Kodi inu simukukumbukira momwe Nimurodi, wachinyengo uja, anamangira nsanja yaikulu iyi ndi kupanga timizinda tina tonse tating'ono tija kuti tizilipira mitulo kwa iwo? Babble ndi Babel ndi chinthu chomwe chomwecho. Iye amangosintha maina ake, ndi, pamene iye akukwera mmwamba. Ndi, Roma tsopano ndi Babeloni. Ndipo dziko lonse likubweretsedwa ku Babeloni, ndipo ilo labweretsedwa ndi Mgwirizano wa Mipingo ya Dziko lonse umene uti udzapange wina aliyense wa iwo kugwadira kwa iye. Ndipo inu mwatengapo chilemba cha chirombo, musakudziwa chimene inu mukuchita. Chifukwa . . .

Koma iwo amene ali osankhidwa adzamva Mawu ndipo adzatulukako kwa izo.

126 Ndi chotsutsana bwanji chipembedzo ndi Mawu a Mulungu! Iye sanayambe wakhalapo ndi chimodzi, sanayambe wachitapo ndi chimodzi, ndipo sanayambe wachitapo ndi chimodzi. Ine ndikufuna wazambiriyakale wina kuti andisonyeze ine pamene mneneri anayamba watulukapo kuchokera mu mpingo. Mundisonyeze ine pamene Mulungu anayamba wadalitsapo mpingo umene unali . . . iwo utatha kuchita bungwe. Iwo umapita pa alumali ndipo umafa, ndi nzeru zaluntha zochokera kwa mdierekezi, ndi atsogoleri awo, ndipo amakana Mawu a

Mulungu pamene Iwo amakula kudzakhala thunthu langwiro la Khristu. Tsopano iwo uli pamutu. Ndi zotsutsana bwanji!

Lekanani ndi Eva wosakhulupirira uyo, inu ana a Kuwala kwa madzulo!

127 Satana, mulungu wa m'badwo uno, mwa chidziwitso chake, akuwapangitsa anthu kuti azidya kuchokera mu mtengo wake wosakanizikana wa chabwino ndi choipa. Zindikirani, Satana, mwa chidziwitso chake, akuwapangitsa anthu a m'badwo woipa uno kuti azidya kuchokera mu mtengo wake wa chabwino ndi choipa. Iye akunena kuti akumanga chitukuko chachikulu cha Chikhristu, mwa chidziwitso chake cha chabwino ndi choipa, chitukuko chachikulu cha Chikhristu.

128 Koma Namwali wamng'ono wa Khristu, Mawu, Gulu, Mkwatibwi, sakusamala za chidziwitso chake. Iye amatalikirana, naye, kutali ndi iye. Ndi chiyani . . . Tsopano tiyeni tikambe za Iye, miniti. Iye akuwadikirira Ambuye Wake ndi kusangalala Kwake kwa Mzakachikwi, kulondola, limodzi ndi Mkwati wa Mawu, monga Iyenso ali Mkwatibwi wa Mawu.

129 Chidziwitso ndi chitukuko, ndi Chikhristu choona, ziribe kanthu kofanana. Chitukuko, ndi Chikhristu choona, ziribe chinthu chimodzi chofanana.

Chitukuko ndi cha mwa chidziwitso. Ife tonse timadziwa zimenezo. Ndipo chidziwitso ndi chochokera ku Edeni, tinatsimikizira zimenezo, ndi zimene iye analalikira mu Edeni. Ndipo chidziwitso chimapangitsa imfa. Ndi kulondola uko? Ndi chiyani chinayambitsa imfa mmunda wa Edeni? Chidziwitso. Koma icho sichingakhale cha Mulungu, chotero icho ndi cha mdierekezi. Psyi, kodi icho chinali chabwino! Chidziwitso, sayansi, maphunziro, ndi cholepheretsa chachikulu chimene Mulungu anayamba wakhalapo nacho. Icho ndi cha mdierekezi.

Tsopano ine ndilandira makalata ena pa zimenezo, ine ndikudziwa. Ine ndikuwadikirira iwo.

130 Taonani chimene chitukuko chatilowetsamo ife. Mukuona? Taonani chimene icho chachita. Kodi ife tiri pati? Ife tatsamira kwa zinthu zimenezo, kudzera mu kumvetsa kwathu kwathu mwa sayansi.

Inu mukuti, "Nanga bwanji Mulungu, kodi inu mukuganiza kuti Iye ndi wosadziwa?" O, ayi.

Mulungu adzakhazikitsa mtundu Wake Wake wa chitukuko pa dziko lapansi, pamene Iye ati adzalitenge ilo. Ili ndi dziko la Satana; iyeyo ndi mulungu tsopano wa chidziwitso chake cha sayansi. Koma Mulungu adzakhazikitsa chitukuko cha mtundu Wake Wake. Icho sichidzakhala chitukuko chonga ichi. Inu mukumbukire zimenezo. Icho sichidzakhala chitukuko cha mtundu umene ife tiri nawo lero. Ayi, ayi. Icho chidzakhala molingana ndi Mawu Ake ndi cholinga Chake. Chifukwa,

mulungu wa m'badwo woipa uno adzawonongedwa, ndi ufumu wake limodzi naye.

131 M'badwo wamakono uno wokonda chidziwitso sukadakhala ndi mtsogoleri wabwino kuposa uyo yemwe iwo uli naye, Satana, wopotoza wa Mawu a Mulungu, monga iye anayambira mmunda wa Edeni, koma munthu wachipembedzo kumadalira pa kumvetsa kwake kwake.

Monga ine ndinanenapo mmbuyomu, Miyambo 3:5, kuti, "Ife tisamatsamire pa kumvetsa kwathu kwathu."

Iwo ayenera kukhala ndi mulungu, chifukwa iwo ndi anthu. Komabe, iye amawapanga iwo chimene iwo akufuna. Monga pokhala anthu, nthawizonse, anthu onse . . . Pamene ife tinkabwera kuno, ife tinawapeza Amwenye akupembedza mafano, ndi dzuwa, ndi chirichonse. Pokhala anthu, iwo ayenera kukhala ndi mulungu. Kotero m'badwo wawukulu uno waluntha uyenera kukhala ndi mulungu, kotero izo zafika . . . Mulungu wa dziko lino wasandulika kukhala chidziwitso, chipembedzo, sayansi, "okhala nawo mawonekedwe a chipembedzo, koma kumakana Mphamvu yake."

132 Zindikirani, mulungu wawo akuwapanga iwo kukhala basi chimene iwo akufuna. Iwo akumasilira za thupi, ndipo ndi chimene iye akuwapatsa iwo. "Iwo amafuna kuti azivala zamkati. Asiyeni iwo azivala izo. Mukuona? Ngati iwo akufuna kuti achite *izi* kapena *izo*, asiyeni iwo achite izo. Mulibepo chovuta chirichonse mu zimenezo; iwo amapita ku tchalitchi. Amayi awo anali a Methodisti, Baptisti, Pentekoste, Presbateria. Asiyeni iwo okha."

Ameneyo ndiye mulungu wa m'badwo uno; wophunzira, wanzeru, wasayansi. Izo sizikusowa chikhulupiriro ayi. Izo sizikusowa kutsimikizira chirichonse. Izo zinatsimikiziridwa kale, mwa chidziwitso chawo. "Chabwino, ndife tchalitchi chachikulu kwambiri chimene chiripo mu tawuni," chidziwitso chawo. "Abusa athu ali ndi D.D., Ph.D." Mwaona, sizikusowa chikhulupiriro chirichonse; amadalira pa chidziwitso. Kuwasiya iwo kuti azikhala moyo mulimonsemo, bola ngati iwo amabwera kudzampembedza iye mwa chipembedzo chawocho ndi kachikhulupiriro. Kuli diso lalikulu lakuda kumeneko, koma yang'anani pa ilo.

Amawaseka Mawu a Mulungu, amanena zinthu zotsutsana ndi Mawu; ndipo amayesera, mwa chidziwitso chawo, kuti akatsimikizire mwasayansi kuti Mawu si owona. O, ndi m'badwo bwanji umene ife tiri nkukhalamo! Mwamuwona mulungu wa m'badwo uno?

133 Zindikirani, koma Mulungu akudikirira kufikira kusaeruzika kwa Aamori wamakono uyu kudzadze. Musadandaule, Iye adzakhala naye Mose Wake atakonzeka pa nthawi imeneyo. Padzakhala kutuluka, tsiku lina, waku

dziko lolonjezedwa. Adzakhalapo Mose ati adzabwere, yemwe ati adzaitane atuluke, "adzabwezeretsa Chikhulupiriro cha ana kubwerera kwa atate." Izo zidzafika, limodzi la masiku amenewa. Kodi . . .

Inu mukuti, "Chabwino, taonani momwe ife tikupitira patsogolo."

Ndithudi, kusaeruzika kwa Aamori sikunadzazebe. Izo zidzachitika, limodzi la masiku amenewa. Asiyeni iwo adziwononge okha.

134 Chitukuko, chidziwitso, kupotoza Mawu a Mulungu kuti agwirizane ndi zokonda zawo zawo. Chipembedzo chirichonse chikuchita chinthu chomwe chomwecho. Satana ndiye akulalikira uthenga wake wake wa chidziwitso mu mpingo wake.

135 Alipo magulu awiri okha a anthu amene akuyankhulidwa mu Chipangano Chatsopano. "Ana a Mulungu, ndi ana a mdierekezi." Kodi inu mumadziwa zimenezo? Inu mukufuna kuti mulembe Lemba la izo? Yohane Woyamba 3:10, ngati inu mukufuna Lemba. Ine ndikuwerenga izo pomwe apa, ndinazilemba izo. Chabwino. Chabwino.

136 Mu Aefeso 2:2, iwo amatchedwa, "Ana a kusamvera." Monga Eva anali, kusamvera ku Mawu a Mulungu. Ana a kumvera, ndi akusamvera, samakhala pa ubale.

Ndiye zingatheke bwanji kuti Mkwatibwi wa Khristu aziyanjana ndi chipembedzo, pamene winayo ndi wosamvera ndipo winayo ndi womvera? Zingatheke bwanji wina, kukhala Mawu; ndipo mmodzi winayo, mawu opotozedwa? Zingatheke bwanji kuti wachiwerewere ndi mkazi wabwino bwino ayendere limodzi? Iwo sangathe kuchita zimenezo. Iwo samayanjana nkomwe. "Tulukani pakati pawo!" Izo ndi za mdierekezi. Icho ndi chilemba cha chirombo. Alunjika wa kumeneko tsopano; zipembedzo zonse. Ine ndiribe nazo ntchito kuti ndi chandani.

Mulungu akutenga, osati chipembedzo, "anthu a Dzina Lake." Chipembedzo sichingalandire Zoonadi izi. Izo zidzatengera munthu payekha yemwe angathe kumuwona Mulungu, kuyang'ana pa Mawu Ake ndi kuwakhulupirira Iwo, ndipo nkusakhala wa bungwe lirilonse; koma kumakhalira moyo Mulungu, osati bungwe lake, luntha la chidziwitso la bishopu wina kapena chinachake zaphunzitsa izo. Uko nkulondola.

137 Ana a kusamvera, ndi ana a kumvera, alibe kanthu kofanana. Winayo wa . . . ndi wa tsiku la Kuwala; mmodzi winayo, wa usiku ndi mdima, m'badwo woipa, m'badwo woipa uno wa mdima, mabala, kuvina, komabe nkukhala a mpingo. Ndi zabwino ndi mulungu wawoyo. Iwo alibe chowatsutsa chirichonse za izo; palibe chimene chimawavutitsa iwo.

"Bwanji, izo sizimanditsutsa ine kumeta tsitsi langa," mkazi anatero. "Sizimapweteka chikumbumtima changa." Iye alibe nkomwe chikumbumtima monga momwe njoka ilibe chiuno. Izo nzoona. Ndithudi ayi. Iye sadziwa kuti chikumbumtima ndi chiyani. Icho chinalochedwa zolimba kwambiri mpaka iye samadziwa kuti ndi chiyani. Uko nkulondola.

138 Kumawalambalala, Mawu a Mulungu, kumati, "Bwanji, zimenezo ndi zachikale zina zopusa. Musamapite kumeneko; iwo angokhala basi gulu la phokoso ndi zotengeka, mulimonse." Huh! Sadziwa nkomwe za Mulungu kuposa momwe Nkafula angadziwire za usiku wa ku Igupto. Uko nkulondola. Izo nzoona.

"Okhala nawo mawonekedwe a chipembedzo, koma kumakana Mphamvu yake; kwa oterowo muchokeko. Pakuti uwu ndi mtundu umene umapita nyumba ndi nyumba, ndi kutsogolera akazi opusa."

"O, wokondedwa, ndinu, inu muyenera kuti muzichita *izi*. O, wokondedwa, ine ndikuganiza mlaliki wanu wachikale wopusa uko, ngati inu basi. . . O, iwe ungawoneke wokongola utavala 'kini," kapena chirichonse chimene inu mumachitcha chinthucho. "Inu, ngati inu mungamachite zonse *izi*, *izo*, ndi *zinazo*. Bwanji, ndudu pang'ono siingamuvulaze aliyense. Ine ndine wa mpingo, ndipo inu mukudziwa chipembedzo chathu chimawonedwa ngati cha wina aliyense." Inu musamukhulupirire wabodza wakale wodzipenta uyo. Iye akunama kwa inu. Izo nzoona. Inde, bwana.

139 Izo ndi zabwino ndi mulungu wawo. O, iye akuganiza kuti izo ndi zodabwitsa, ndipo iwo amangomukonda iye chifukwa cha izo.

Mai, iwo angatsutsane ndi iwe. Iwo angaimirire ndi kukutsutsa iwe za izo. Bwanji, ndithudi, Satana anaima kumene pamaso pa Yesu Khristu, Mawu, ndipo anayesera kunena kuti, "Kwalembedwa."

Ndipo apo Iye anali, Mawu otsimikiziridwa a Mulungu. Iye anati, "Pita kumbuyo Kwanga, Satana!" Anangoyenda ndipo anakachita chinthu chomwecho.

Monga munthu ananena ndi ine nthawi ina, anati, "Tsopano, ngati inu mukukhulupirira ubatizo wa Mzimu Woyera ndi wolondola, ndipo inu mukukhulupirira kuti inu muli nawo Iwo," anati, "tsopano inu mundikanthe ine ndi khungu." Ameneyo anali mlaliki. Anati, "Inu mundikanthe ine ndi khungu!" Iye anati, "Paulo anamukantha—munthu ndi khungu tsiku lina."

140 Ine ndinati, "Bambo, ine ndikukanthani bwanji inu ndi khungu pamene ndinu wakhungu kale? Ine ndikuphani bwanji inu pamene ndinu wakufa kale?" Uh-huh.

Iye anati, "Ine, maso anga ali twente-twente!"

Ine ndinati, "Gawo lanu la thupi; koma inu mukadali wakhungu."

"Ndi zosatheka! Baibulo silimatanthauzira zinthu. Ife timalankhula pamene Baibulo lalankhula, ndipo chete pamene Ilo liri chete."

141 Ine ndinati, "Chabwino, pamene Eliya anali uko—ku Dotani, mwaona, uko kunabwera ankhondo onse a Asiriya atawazungulira. Ndipo wantchito anathamangirako, anati, 'O, bambo anga!' Anati, 'Bambo anga,' anati, 'Asiriya atizungulira ife.'"

"Eliya anatikita maso ake, anadzuka ndipo anati, 'Alipo ochuluka amene ali ndi ife kuposa amene ali ndi iwo.'"

"Iye anati, 'Ine sindikuwonapo aliyense.'"

"Anati, 'Mulungu, mutsegule maso ake.' Tsopano, iye anali wakhungu. Ndipo iye anayang'ana pozungulira mneneri wokalamba uyo, ndi pa mapiri; panali patadzaza Angelo, ndi magaleta a Moto, ndi akavalo a Moto."

"Ndipo iye anayendera kumeneko, ndipo Baibulo linati, 'Iye anawakantha iwo ndi khungu.' Khungu kwa chiyani? Kwa iye. Iye anayendera kumeneko, anati, 'Kodi inu mukufunafuna Eliya?'"

"'Inde, ife tikumufunafuna iye.'"

"Anati, 'Kazibwerani, ine ndikusonyezani inu kumene iye ali.' Eliya akuwatsogolera iwo kwa Eliya. Khungu!"

Ine ndinati, "Inu mukudziwa chimene ine nditi ndinene kwa inu? Ndendende basi chimene Ambuye wanga ananena kwa atate anu, 'pita kumbuyo kwanga.'" Uh-huh. Uh-huh.

142 Zindikirani, ana omvera, ndi akusamvera, samakhala paubale. Wosamvera amapembedza mulungu wawo. "O," iwo amati, "ife timakhulupirira Baibulo." Inde, iwo ndi mtengo wosakanizikana. Mwaona, iwo amawonjezera chidziko ndi chidziwitso kwa Iwo. Mtengo wa Satana, utasakanizikana; mwaona, iye anatenga kuchokera ku mtengo wa Satana, chabwino ndi choipa. "O, ife timakhulupirira Mawu." Ndithudi, koma osati onse a Iwo. Eva anakhulupirira Mawu, nayenso, koma mulole—mulole Satana atenge mtengo wake ndipo awupotoze Iwo pang'ono pokha. Ndicho chimene izo ziri.

"Aliyense amene adzawonjezera mawu amodzi, kapena kuchotsapo Mawu amodzi kwa Awa." Iye akadali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Zindikirani. Chabwino.

143 M'badwo woipa uno ndi wa mdima, komabe nkukhala wa mpingo. Mulungu wawo, iwo amamukonda iye chifukwa cha izo, momwe iye amawasiyira iwo kuti azichitira izo. Iwo alibe chowatsutsa. Palibe kalikonse kamawatsautsa iwo bola ngati iwo ali a mpingo.

Balaamu anawuphunzitsa mpingo chinthu chomwecho. "Tiyeni ife tiyanjane; ndife tonse ofanana." Iyo inali ndale yotsiriza. Mulungu sanawakhululukire iwo nkomwe pokhulupirira bodza loterolo.

144 Kumbukirani, ilo linali tchimo losakhululukidwa, katatu mu Baibulo, munthu aliyense akawonjezera mawu amodzi a kutanthauzira kwawo kwawo ku Mawu a Mulungu Iwo atatha kale kutsimikiziridwa kuti ndi Choonadi.

Mmunda wa Edeni, kumene, mmunda wa Edeni, mawu amodzi atawonjezeredwa zinayambitsa imfa.

Pamene Balaamu anawonjezera mawu, akuti, "Ndife tonse ofanana," iwo, Mulungu sanakhululukire nkomwe Israeli chimenecho. Mmodzi aliyense wa iwo anafera mu chipululu, kupatula atatu amene Mulungu anawatulutsa.

Yesu anati, "Iwo ali, mmodzi aliyense, anafa," ndiko kulekana Kwamuyaya. Iwo onse anapita; sanakhululukidwe nkomwe. Ilo ndi tchimo losakhululukidwa; sanawakhululukire iwo nkomwe. O, mai!

Thawani izo, ana a Kuwala kwamadzulo!

145 Mwamuwona tsopano yemwe ali mtsogoleri wa m'badwo wamakono uno, wachipembedzo, woipa? Iyeyo ndi mdierekezi, watenga mtengo uwo wa chabwino ndi choipa, ndipo wakawuika iwo kunja uko, mwaona, wawubweretsa mpingo wake wa mkwatibwi wokongola ku ecumenical council ku chikwati. Ndi chabwino chimenecho. Mpingo wake wokongola wa sayansi, ndi madigirii o—o—onse amene angathe kupezedwa; ma Ph.D kuchokera mu mpingo wa Khristu, ma Ph.D kuchokera mwa Baptisti, Presbateria, Pentekoste, ndi onse. Kuwabweretsa iwo onse, ndi zipala zawo zokongoletsedwa ndi matchalitchi akulu akulu, onse waku ecumenical council, "Ndife amodzi." Izo sizidzakhululukidwa nkomwe. Chipembedzo, kuvala dzina la chipembedzo, ndi chilemba cha chirombo. Ife tadutsamo mu zimenezo kuno; kuchita zimenezo. Thawani izo, ana, thawani izo! Mukuona? Mpingo wawukulu, wokongola wovala za ecumenical, kuvala chilemba chake!

Akabudula, ndithudi, zovala zachidziko, zokhumbitsa kugonana, penti, ophunzira abwino kwenikweni a mdierekezi, kuti akawagwire ana aamuna a Mulungu; kukamukwatitsa mnyamata wabwino wobadwa mwathunthu kwa wapathengo wina ngati ameneyo. Izo nzoona. Chiyani . . .

146 Inu munati, "Kumeta tsitsi, zimenezo ziri ndi chochita chanji?"

M'bale, tiyeni tiimikire apa miniti chabe. Ine ndikungomverera winawake akuchikana chimenecho. Mwinamwake ali kunja pa lamya kwinakwake.

Tamvetserani. Tsitsi kwa mkazi ndi lumbiriro la Unaziri. Tsitsi kwa Samson linali lumbiriro la Unaziri. Ndipo pamene mkazi adula tsitsi lake, iye—iye mwamtheradi amakana lumbiriro lake la Unaziri kuti iye ndi Mkwatibwi wa Khristu. Chifukwa, apo, chinthu chimodzi chimenecho, iye akuwononga Chithunzi chonsecho. Kukhoza! *Mnaziri* ndi "mmodzi amene ali wopatulidwira cholingacho." Ndi kulondola uko? Samson anapatulidwira ku m'badwo ndi kwa cholinga, chotero iye anali ndi tsitsi lalitali. Mkazi yemwe ali mwana wa Mulungu, amalisiya tsitsi lake kuti lizikula, kuti akasonyezere kuti iye ndi wopatulidwira ku Mawu aliwonse a Mulungu.

147 Ngati iye alidula ilo, ine ndiribe nazo ntchito kaya iye amavina mochuluka bwanji, amaimba, ali mu kwayala, amalankhula mmalirime, amathamanga chokwera ndi chotsika, kapena ali ndi mitundu yonse ya magulu a zithandizo, iye ndi wakufa. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE, Mawu a Mulungu. Akorinto Woyamba 14. Eya. Iye wakana lumbiriro lake la Unaziri ndipo wadzigulitsa kwa mulungu wa m'badwo wamakono uno. Iye akuchita zimenezo. Tsopano, manyazi pa inu, dona, kapena mkazi!

148 Ogwira enieni a ana aamuna a Mulungu, monga izo zinali. Monga Yesu anati, "Monga mmene zinali mu masiku a Nowa, kukongola kwa akazi, ndipo ana aamuna a Mulungu anayamba kukwatirana pakati pawo, chomwechonso izo zidzakhala pamene Mwana wa munthu azidzabwerera." Ndipo mulungu wawo amaganiza kuti ndi zopambana, ndi zokongola, ndi zasayansi, chidziwitso; fashoni ya Hollywood, zokonzedwa mu shopu yake yomwe, ndithudi, zonse izi apa zobaya ndi zinthu, inu mukudziwa.

149 Ndipo iye, mpingo wake, umazikonda basi zimenezo! O, mai! "Ine ndidzakupatsani inu kuti mumvetse, ndine wa Methodisti. Ndine wa Presbateria. Abusa athu amaganiza bwino sanganene chinthu ngati chimenecho." Iye alibe kuganiza kwabwino kuti azinena zinthu zimene Mulungu amanena ndiye. Mukuona?

150 Iye, mpingo, umangopembedza izo. Iye amazikonda izo. Basi ndi zimene iye amafuna! Iye sangajowinane ndi kalikonse, m'bale, kapena kubwera mu chirichonse iye ayenera kuti azichita chinachake mosiyana ndi chimene Ayezebeli amakono awa ali, chifukwa ndicho chikhalidwe chimene chiri mwa iye.

Iwe ungathe bwanji kukhala chikhalidwe chirichonse... "Nanga potenga lingaliro angathe kuwonjezera gawo limodzi pa thunthu lake?" Ngati iwe unabadwa kuti udzakhale wamtali mapazi asanu, iwe sudzakhala mapazi sikisi. O, eya, monga "makina ofunyululira" a Booth-Clibborn.

151 Ndiye tamvetserani, bambo, inu gulu la marickie! Ngati inu munabadwa kuti mudzakhale mwamuna, ndiye kazichitani ngati mwamuna. Matsitsi opota awa akulendewera pansi pa

nkhope yanu, ndi lopotedwa ngati mawonekedwe ena a kudolola kofuna kugonana, bwanji, inu kam'badwo kopotozedwa ka njoka! Vuto ndi chiyani ndi inu, mulimonse?

Mulungu wanga adzaliweluza fuko lino tsiku lina ndi moto. Iye adzalimizira ilo pansi pa nyanja. Ora la chiweruzo Chake liri pafupi. Dziko lonseli lidzapita.

152 Kupotoza kwa chipembedzo! Kupotoza kwa umunthu; amuna osadziwa nkomwe kuti ali mbali iti, chomwechonso akazi. Kuimirira atavala ovololo, kapena kabudula wakale wamng'ono, zovala zimene. . . kusuntha kwake kulikonse ndi mawumbidwe a thupi lake, ndipo nkumadzitchula yekha Mkhristu. Iye siali nkomwe dona, ndiye mukunena zakukhala Mkhristu. Iye ndi wachiwerewere wa pa msewu wogwiritsidwa ntchito ndi Satana, wodzozedwa ndi Satana, kuti akatumize ana aamuna a Mulungu wa ku gehena, kuti akakwaniritse Mawu amene Yesu Khristu anati akanadzachitika. Ine sindimatanthauza kuti ndinene zimenezo, koma Iye ananena zimenezo, mulimonse. Kodi mukuona kumene mzimu uwu wachipembedzo ukuchokerako? Mtengo wosakanizikana.

153 Mukuti, "Chalakwika ndi chiyani ndi zazifupi zimenezo," kapena chirichonse chimene iwo amadzitcha izo, "ngoleka?" kapena chirichonse chimene izo ziri.

Baibulo linanena, kuti, "Mkazi aliyense amene ati adzavale chovala choyenera mwamuna, ndi themberero pamaso pa Mulungu." Ndizo PAKUTI LITERO BAIBULO.

Ndipo mkazi yemwe angadule tsitsi lake, amanyazitsa mutu wake. Ndipo siziri nkomwe. . . Ndi chinthu chochimwa kuti mkazi apemphere ndi tsitsi lalifupi, Baibulo linanena chomwecho, kupemphera pagulu ndi mutu wosaphimba. Ndipo iye. . .

O, inu mukuti, "Ine ndimavala chipewa."

154 Iwe wachinyengo, kumawaphunzitsa akazi awo zinthu zoterozo! Pamene, Baibulo linati, "Tsitsi lake linaperekedwa kwa iye ngati chophimba," osati chipewa chopangidwa ndi munthu. Ndi zimene Baibulo linanena. Ine ndiribe choyankhira; ine ndiri nacho choyankhira ponena Choonadi. Musakhale wosawona mtima, monga Baibulo linanenera, "Kuwagwira Mawu a Mulungu mwachinyengo," ku—kukonza kapena—kapena kukomana ndi chopempha cha gulu la maricketta.

155 Ine ndiri ndi mawu akuti *woipa* apa. Ine ndinalemba kuti "Elvis" mmalo mwa *woipa*. Zonsezo ndi zofanana. Mawu akuti *Elvis* amatanthauza "khoswe," ndipo mawu akuti Ricky amatanthauza "khoswe." Pamene inu munena kuti "Ricky" wamng'ono, inu mukutanthauza "khoswe wamng'ono." Chimene inu mumamutcha iye, ndicho chimene iye ali. Mwana

wanu amatchedwa chimenecho, mulisinthe ilo mwamsanga, chifukwa cha Uthenga. Musamutchule dzina mwana . . .

Inu simunayambe mwamvapo maina oterowo mmbuyo mu Baibulo, kapena mu m'badwo wina uliwonse. Ndi m'badwowo, dzina la m'badwo uno. Ngati panayamba pakhalapo makoswe ndi amphaka opotozedwa, ndi pamenepo.

156 Zonse izi . . . ? . . . oyika zimbale za nyimbo za millioni dolla, ndipo ana awa kumayenda kuno, osatha ngakhale kupita ku—ku sukulu opanda kanthu katamatidwa pa khutu lawo, ndi kawailesi kakang'ono kakale kali mthumba mwawo, basi, "kakuphokosera."

O, iwo anabwera ku nyumba uko, ndipo ife timapanga . . . Anyamata amenewo amayesera kuti apente nyumba yanga kumeneko. Ife tinati, "Chotsanipo chinthu chimenecho apo. Ngati inu simungathe kugwira ntchito popanda chimenecho, ndiye isiyeni ntchitoyo. Zimandipangitsa ine kukhala wamanjenje kwambiri ndimalephera ngakhale kuti ndiime pano. Ife tinawapereka malo ano kwa Mulungu. Ife sitimafuna mtundu uwo wa zamaphokoso zamkhutu za masiku otsiriza ano pamalo pano." Ine ndinati, "Chizimitseni icho kapena isiyeni ntchitoyo!"

157 Zindikirani, achipembedzo, ngakhalebe, o, ndithudi, amapita ndithu ku tchalitchi ndipo amakaima pakhomo, ndi kumamvetsera gwedemula.

158 Ndiponso, zindikirani, Mkwatibwi wa Mawu a Khristu akupita, nayenso. Pamene ife tikuwona kumene wotsutsakhristu akupita, anayambira kumbuyo uko ndipo tsopano akufika ku mutu; ecumenical council idzaziyika izo ku mutu wa zachipembedzo. Ndipo Mpingo wawung'ono umene wabwerapo, nawonso, Mkwatibwi wa Mawu wa Khristu kudutsa mu m'badwo, akubwera ku Mutu, chifukwa Iye alumikizidwanso ndi Mwamuna Wake. Nthawizonse, chimodzimodzi monga mpingo ndi china chirichonse, Iye ayenera kulumikizidwa. Tirigu, china chirichonse, zikubwereranso ku mutu wake kumene icho chinayambira; monga Kaini ndi Abele. Mkwatibwi wa Mawu walunjika mmwamba mwa Munthu wa Mawu a Mulungu atasandulika thupi mu m'badwo woyipa uno umene ife tiri nkukhalamo. Kodi mukuona kumene izo zikupita?

159 Ndipo Satana posachedwapa amutenga mkwatibwi wake waluntha ndipo amukweza wamkulu uyu, amene ali wotsutsakhristu, kulowezana mmalo, ndipo adzamukhazika iye pa mpandowachifumu, "ndipo dziko lonse lidzazizwa likumutsatira iye."

Ndiyeno Khristu adzabwera. Ndipo awiriwo sizingatheke kukhalapo nthawi imodzi. Ndipo ufumu wake udzachotsedwapo; iye adzawonongedwa.

Ndipo Khristu, Mawu a Mulungu . . . Chimene, mkazi ndi gawo la thupi la mwamuna. Iwowo si awiri; iwo ali mmodzi. Ndipo Mkwatibwi, Mpingo, Mawu, "anthu oitanidwa atuluke kuchokera *apa* ndi *apo*, chifukwa cha Dzina Lake," adzalumikizana mu Thupi la Yesu Khristu.

Ndipo ufumu wa wotsutsakhristu udzachotsedwapo ndipo udzawonongedwa. Ndipo Khristu adzatenga mpandowachifumu, ndipo adzakhala pa mpandowachifumu wa atate Ake Davide, ndipo adzalamulira pa dziko lapansi kwa zaka chikwi; kenako adzaupereka Mpingo kwa Mulungu, "wopanda banga kapena chilema." Inde!

160 Tsopano zindikirani tsitsi lake lalitali, lumbiriro la Unaziri ku Mawu. Ine ndimujambula Mkwatibwi wa Khristu tsopano. Ife timujambule wotsutsakhristu, kumene iye ali, wachipembedzo ndi chirichonse, sayansi. Tsopano Mkwatibwi wamng'ono wodzichepetsa wa Khristu mophweka amangokhulupirira Mawu, yense yemwe Iye ali. Ndi aliyense payekha. Ine ndikuyembekeza ndipo ndikudalira kuti alipo ambiri amene akhala pano, ambiri akumvetsera. Ndipo ine ndikuyembekeza kuti inemwini, ndi aliyense wa inu nonse, ndinu gawo la Mkwatibwi ameneyo. Ine ndikuyembekeza ambiri. Ndipo, izo zidzakhala, onse amene anadzozedwera chimenecho adzakhala chimenecho, chifukwa ndicho chikhalidwe chawo. Iwo amawona. Mawu akhoza kungozindikira Mawu. Iwo sangathe kuzindikira chipembedzo kapena kupotoza. Iwo amadziwa bwino; Iwo ndi Mawu. Mukuona? Iwo sangathe kuzindikira chirichonse . . .

Tirigu sangakhale chirichonse koma tirigu. Iye anayamba, tirigu; iye adzathera kukhala, tirigu. Ndipo maudzu sangathe kukhala tirigu, komabe iwo amathiriridwa ndi kudzoza komweko. Mukuona? Koma iwo si tirigu. Monga ine ndinanena tsiku lina, zokhudza mtengo wokhala ndi nthambi zosiyanasiyana pa iwo.

161 Tsitsi lake lalitali, lumbiriro la Unaziri, limasonyeza kuti Iye analumbirira kwa Mulungu. Chovala chake chokongola cha Mawu Ake olonjezedwa a m'badwo umene Iye ali nkukhalamo, chitakulungidwa pa Iye, kumutsimikizira Iye ndi Iyemwini, wa Ahebri 13:8, "Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Monga, Iye ali gawo la Mkwati wa Mawu, woona kwa Iye mu nsonga iliyonse.

162 Tsopano taonani. Ngati mkazi apita kuno ndipo nakakwatira ndi mwamuna, ndipo iye nachokako ndipo nakapanga chikondi ndi mwamuna wina ndipo nkukhala pa chibwenzi ndi iyeyo, ndipo nabwereranso kwa mwamuna wake, mwamunayo ayenera amuthamangitse iye. Nkulondola uko? Mkaziyo ayenera kukhala woona kwa iye, chifukwa iye analumbirira kwa mwamunayo.

Ndipo Mkwatibwi wa Khristu analumbirira kwa Khristu; ndipo Iyeyo ndi Mawu.

Asamatsinzinire nkomwe kwa enawo, mkazi asamatsinzinire pa mwamuna wina. Iye asamapange zizindikiro zirizonse, asamakhale ndi kutengeka kulikonse pa mwamunayo, chifukwa iyeyo mwamtheradi ndi mkwatibwi kwa mkwati mmodzi.

163 Ife sitikufuna uliwonse wa mitengo yanu yosakanizikirana, zipembedzo zanu. Mukhale woona kwa Khristu, Mawu. Iye adzawatsimikizizira Iwo kuti ndi owona. Ayi, bwana, asamakhale nkomwe ndi kutengeka kulikonse kwa chirichonse cha kupanga chikondi kwa mwamunayo, osati kukalowa mmabwalo ake kapena china chirichonse, kapena kumulola iye kuti akukumbatire iwe mmikono yake kapena mu chisamaliro chake, kapena—kapena kulankhula nawe mwanjira *iyi*, njira *iyo*.

Iwe udzimvetsera kwa Liwu limodzi lokha. "Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa. Mlendo izo sizidzatero . . ." Kodi Liwu Lake ndi chiyani? Liwu la mwamuna aliyense ndi mawu ake. Ndipo izi ndi Ilo, Baibulo, mawu amodzi asawonjezeredwe kwa Ilo kapena kuchotsedwapo kwa Ilo. Muzingokhala limodzi ndi Liwu limenelo. "Mlendo iwo sangamutsatire," chipembedzo.

164 Monga, Iye ali gawo la Mkwati, woona kwa Iye mu nsonga iliyonse, kuyembekezera Chikwati. Kulumikizana, osati ku ecumenical council; koma mu mlengalenga, pa Mgonero wa Chikwati. Iye wapatsidwa . . . Izi ndi za mpingo wathu wathu. A . . . Iye wapatsidwa, ndipo wawulula kwa Iye, zinsinsi za Chisindikizo cha Chisanu ndi chiwiri za Baibulo. Mukuona? Iye akuwona kupusa kwa wonyengayo, zoyandikira kwambiri ndi Choonadi, mwakuti pafupifupi akananyenga Osankhidwa. Iye akuwona zimenezo. Iye . . .

165 Mukuiwona mizimu iwiri yotsutsayo imene ili pa ntchito mu m'badwo woipa uno? Kodi inu mukutha kuiwona iyo? Uliwonse wachipembedzo kwambiri, Kaini ndi Abele, mizimuyo kachiwiri ikufika ku mitu yawo, chimodzimodzi basi monga iyo inayambira. Wina, wopembedza mwa kukongola, ndi mwa chidziwitso, ndi mwa maphunziro, ndi mwa sayansi, ndi mwa mbalume. Ndipo Winawo, mwa chikhulupiriro cha vumbulutso la Mawu a Mulungu. Iwiri yonse ya iyo ikuimirira mu nyumba ino mmawa uno. Ndiko kulondola.

166 Vumbulutso, kapena chikhulupiriro, mu Mawu Ake, samadzinenera za chidziwitso; Mkhristu weniweni, woona.

Iwo amati, "Kodi inu muli ndi—inu muli ndi digirii ya udokotala?"

Samapanga kudzinenera. "Ine—ine ndikukhulupirira Mawu Ake." Mukuona? Samapanga kudzinenera kulikonse. Samadzinenera kuti ndi wophunzira. Si wa chipembedzo

chirichonse, gulu lirilonse, gawo lirilonse. Iwo ndi a Khristu. Iyeyo ndi Mkazi Wake; osati mkazi wa mpingo.

Iye ndi wachiwerewere. Baibulo linati iye anali "hule," ndipo, "MAYI WA TIMAHULE," ndipo iwo onse akubwera pamodzi ndipo akudzapanga hule lomwelo. Ndipo mkazi wa mtundu umenewo ndi mkazi yemwe si woona kwa Mwamuna wake; ndipo amadzinenera kuti Khristu ndi mwamuna wake, ndipo ndi wa chipembedzo. Zamkhutu zoterozo! Ife tiri a Khristu.

167 Koma, mu kumvera, Mkazi wa chikhulupiriro chaching'ono uyu, yemwe amakhala moyo mwa chikhulupiriro, Mkwatibwi; munthu *apa*, *apo*; apa, wochokera kwinakwake, mpingo winawake, chipembedzo chinachake, chirichonse chimene icho chiri, mwa ena ayi . . . Amakhulupirira Mawu a Mulungu, womvera, amadikirira mwa chikondi, kuti lonjezo la m'badwowo likwaniritsidwe. Iye akuyembekezera ilo. Iye ali gawo la Mawu amenewo, ndipo Iye akuyembekezera kuti moyo Wake uwonetsere Mawu amenewo.

Abale, kodi inu simukutha kuwona zimenezo? Ine ndikudalira kuti zimenezo sizinakulambalaleni inu.

Thupilo likudikirira (limene liri Mawu), likudikirira Moyo (umene uli Mzimu) kuti ukatsimikizire kapena kuwapanga Iwo amoyo. Ndicho chimene Iye akudikirira. Palibe moyo wina umene ungagwire ntchito mwa Iye. Iye sangathe kubwera ku moyo mwanjira iliyonse. Komabe, Iye amamverera izo kumeneko, ndipo Iye amadziwa kuti zidzachitika; ndiye apa izo zimachitika, ndiye Iye amadzuka. Mulungu anati, "Apo pakhale," ndipo Iye anatulukira monga woyamba uja anatulukira.

168 "Ana a kusamvera" zimatanthauza kumvera . . . *Kusamvera* kumatanthauza "kugalukira." Ine ndinayang'ana zimenezo mu dikishonare, kuti ndikhale wotsimikiza. Kugalukira, kugalukira motsutsa (chiyani?) Mawu owululidwa a Mulungu. Monga Kaini anawulula . . . anagalukira motsutsa vumbulutso lowululidwa la Abele, otsimikiziridwa ndi Mulungu kuti ilo linali lolungama. Ndipo Kaini anagalukira motsutsa ilo, ndipo anamupha m'bale wake.

Afarisi, ndi chidziwitso chawo chomwe cha chipembedzo cha chimene Mawu a Mulungu anali, munthu wosankhidwa wotoledwa ndi dzanja, anagalukira motsutsana ndi Mawu otsimikiziridwa a Mulungu owonetseredwa a tsikuli, Yesu Khristu, ndipo anamupha Iye. Kulondola uko?

Ndicho chimene "ana a kusamvera" ali, akugalukira motsutsa Mawu a Mulungu.

Tsopano mukuona kumene iwo ali? "O, masiku a zozizwitsa anatha. Yesu Khristu siali yemweyo panobe. Palibepo chinthu

chotero ngati ubatizo wa Mzimu Woyera. Zinthu zonsezo ndi zamkhutu!" Mwaona, kugalukira! Iwo sakusowa kuti anene zinthu ziwiri; akungoyenera kuti anene chimodzi, ndi zokhazo. Ndiko kugalukira, pomwe apo. Iwo sanganene kuti inu mulibe maso, inu mulibe makutu; inu muyenera kutenga thupi lonselo, Mawu onsewo. Mukuona?

Kuitana kwa Mzimu Woyera, "Tuluka mwa iye, usakhale wotenga nawo za mwambo wake wa chipembedzo," pamene iye akuseka ndi kuwanyoza Mawu a Mulungu a tsiku lino.

"Pakuti Mulungu samaseleulidwa," mungokumbukira. Iye adzalipira izo. Musati mudandaule. Iye adzalipira izo. Baibulo, mu Aefeso 4:30, ngati inu mukufuna kuti mulembe izo, Aefeso 4:30, amatero. "Mulungu samaseleulidwa. Chirichonse chimene munthu afesa, chimenecho iye adzakolola." Iwo sangathe kumuseleula ndi kumuseka, ndi kunena zinthu izi, ndi kumapitirira nazo izo. "Monga mkate pa madzi, iwo udzabwerera."

169 Iyeyo ndi mkwatibwi wa mdierekezi, atakutiridwa mu chipembedzo chake, chidziwitso chokonda tchimo cha m'badwo woipa uno wa lero, kuti adzakunyengeni inu. O, mai! Kagulu konseko kapena chipembedzo cha mizimu yodolola, mwa chidziwitso cha sayansi ndi chitukuko cha makono! Kumadzinenera . . .

Ife titseka mu maminiti pang'ono chabe. Ine ndiyenera kuti ndiimikire, chifukwa ine sinditha kutsiriza zonsezi, mwaona.

Kumadzinenera kuti iye akumanga dziko lalikulu kuti inu muzidzakhalamo. Iye amadzinenera, kuti, mu chitukuko chakecho, iye wamanga matchalitchi abwino, makoleji, masukulu, zipatala, malaibulale, ndi chithandizo cha kanthawi pang'ono cha munthu, popanda Mawu a Mulungu. Iye wachita zimenezo. Iye watsimikizira kuti iye akhoza kuchita zimenezo. Ndipo anthu agwera zimenezo; inde, bwana; masukulu, zipembedzo, chitukuko, anthu ovala bwino, anthu odyetsedwa bwino.

Ine kulibwino ndikhale pa mzere wa buledi, ndi kukhala pa ubale ndi Mulungu; kusiyana ndi kukhala ndi nkhuku yokazingidwa katatu pa tsiku, ndipo nkukhala wa wachiwerewere monga choncho.

170 Kumbukirani, ora liri pafupi pamene chilemba chiti chibwere. Inu mwina mudzakhala mwa izo kapena kunja kwa izo. Ilo lidzafika ngati mbala usiku. Ilo lidzakupezani inu pomwe apo, ndipo inu muli pamenepo. Apo sipadzakhala kuchokako kwa izo pamenepo; inu mwachitenga kale icho. Tulukanimo!

Mngelo anatsika kuchokera Kumwamba, wokhala ndi nkhope yowala, ndipo anafuula mokweza kwa anthuwo. Izo zinagwedeza dziko lapansi. "Tulukanimo mu Babeloni, pakuti

iye wagwa. Musakhale otenga nawo a miliri yake, anthu Anga!" Chokaniko kwa iye. Chokaniko uko! Kodi sitinawerenge kumene izo mu Mawu, kanthawi kapitako? *Mngelo* ndi "mtumiki," mwaona, akutsika pansi. Zindikirani Mzimu Woyera, "Tulukani pakati pake, kuti musakhale otenga nawo."

171 Tsopano iye wamanga zinthu zonsezi. Iye wamanga matchalitchi akuluakulu. Iye wamanga koleji, masukulu, wawatenga anthu ndipo wawaphunzitsa iwo kukhala a—abwino, zotchedwa, chitukuko. Ndipo iwo awaphunzitsa iwo ndi chitukuko chamakono chimene chiwafikitsa iwo mu dzenje la imfa, mwa chidziwitso, kutali ndi Mulungu ndi Mawu Ake.

Kodi inu simukuiwona ndale yonseyo? Kodi inu mukuziwona zimenezo, mpingo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Kunja uko pa wailesi, ngati inu mukuziwona izo mu magulu anu omwe kumeneko, munene "ameni," onse a iwo adziwa pamene inu mwaima. Mukuona?

Iye anachita izo. Iye ali. . .Iyeyo ndi mulungu wa dziko lapansi lino, ndipo iye wamanga makoleji. Iye wamanga maunivesite. Iye wamanga zipatala. Iye wamanga malaibulale. Iye wamanga zinthu zonse izi kwa thandizo la kanthawi kochepa kwa munthu, zongokwanira kuti ziwanyenge iwo, kuti achokeko ku Mawu amenewo. Ndipo kodi iye wawatsogolera iwo ku chiyani? Dziko lonse la mpingo lagwera mu imfa, pakuti Mulungu anati Iye akanadzamuwotcha huleyo, ndi ana ake, ndi moto wosatha.

Tulukanimo mwa izo, anthunu! Musati mugwidwe mmenemo. Inu muchokeko kwa chinthu chimenecho mwamsanga mmene inu mungathere!

Mwa chidziwitso chake cha sayansi, iye wakhoza kuchita izi, tsopano zindikirani, wopanda Mawu a Mulungu.

172 Mulungu sanatidzoze konse ife kuti tizipita uko ndi kumakakhala ndi masukulu. Iye sanatero. Iye sanatiuze ife nkomwe kuti tizikamanga zipatala. Izo ndi zabwino. Iye sanatiuze ife kuti tizikamanga malaibulale. Ayi, bwana. Iye sanatero.

Iye anati, "Mulalikire Uthenga." Ndipo, Uthenga, ndi kuwonetsera mthupi, kuwonetsera mphamvu ya Mzimu Woyera.

Paulo anati, "Uthenga unabwera kwa ife, osati podzera mmawu okha, koma kudzera mu kuwonetsera mthupi ndi mawonetseredwe a Mzimu Woyera." Paulo anati, "Ine sindinabwere konse kwa inu ndi mawu aakulu a nzeru a dokotala wina wotere, koma ine ndinabwera kwa inu mu mphamvu ndi mawonetseredwe a Mzimu Woyera; kuti chikhulupiriro chanu chisakhale mu nzeru kapena chidziwitso cha anthu a dziko lino, koma mu mphamvu ya chiukitsiro cha Yesu Khristu; chifukwa Iye alimoyo, yemweyo dzulo, lero, ndi

kwanthawizonse.” Mulungu atithandize ife kuti tizikhulupirira chinthu chomwe chomwecho, ndipo Mulungu atsimikizire chinthu chomwe chomwecho monga Iye wakhala akuchitira.

173 Iye amakutchingani inu kuti musawone vulumbulutso loona ndi chikhulupiriro cha Mawu a Mulungu akuwululidwa ndi kutsimikiziridwa lero, mwa masukulu ake, malaibulale, mabuku, zipatala, ndi zina zotero. Mukuona? Iye akukutchingani inu kwa izo. Iye tsopano akutanthauzira, monga iye anachitira kwa Farao, kuyesera kuti akutchingeni inu kuti musawone tanthauzo la Mawu otsimikiziridwa a m’badwo Wake wolonjezedwa mu Kuwala kwa madzulo, ovomerezedwa ndi otsimikiziridwa. Iye wayetsetsa, mwa chidziwitso chake, ndi masukulu, ndi anthu ophunzitsidwa bwino, ndi mbalume, ndi zina zotero, kuti akutchingeni inu kuti musawawone Iwo.

Chirichonse, kuchitira kuti inu musayang’ane pa Icho ndi kuwona kuti ndi Yesu Khristu! Inu mungadziwe bwanji kuti ndi Yesu Khristu? Iye ali Mawu, ndipo Iye ali Mawu a m’badwo uno. Ndipo m’badwo uno, anati izi zikanadzachitika mu m’badwo uno, ndipo apa izo zikuchitika. Mukuona? Mukuona? Iye akuyesetsa mwakukhoza kwake kuti akutchingeni inu kuti musawawone Iwo.

Iye adzakhomapo dzina loipa lirilonse pa Iwo mmene angathere. Mukuona? Iye adzawatcha Iwo “oyera-odzigudubuza” ndi china chirichonse. Iye anamutcha Yesu “Belezebule.” “Ndipo iwo amamutcha Mbuye wa nyumba Belezebule, ndi mochuluka bwanji iwo ati adzawatche ophunzira?” Mukuona?

174 Mwaona, kuyesetsa kuti akutchingeni inu kuti musawone tanthauzo lenileni la Mawu. Osati zimene. . .Mwaona, iye akuwatanthauzira Iwo, kumati Iwo amatanthauza *izi*.

Mulungu anati, “Ine ndinalonjeza mmasiku otsiriza kuti Ine ndidzakutumizirani inu Malaki 4.” Izo sizikusowa kuti zitanthauziridwe; Iye anachita izo. Iye anati, “Ndipo monga izo zinali mu masiku a Loti, dziko lidzakhala mu chikhalidwe cha Sodomu; ndipo mu nthawi imeneyo, Ine ndidzamuwulula Mwana wa munthu ndi izo, ndendende.” Ife tiri nayo mitundu yonse ya zotsanzira ndi china chirichonse, cha izo, koma ife tiri nacho Chimodzi chenichenicho, aponso. Mukuona? Iye anati Iye akanadzachita izo.

Iye anati wotsutsakhristu adzauka ndipo pafupifupi kunyenga Wosankhidwa ngati kukanakhala kotheka. Koma anati, “Asiyeni iwo okha. Asiyeni iwo azipitirira. Kupusa kwawo kudzapezeka.” Bwanji? Kuyesa kwa Mawu kumatsimikizira izo. Mukuona?

Pamene izo zifika ku Mawu amenewo, “Amene anakhala ali mmbuyo mbali *iyi*, *iyo*? O, ine sindimakhulupirira mu mbewu ya serpenti. Ine sindimakhulupirira *izi*, *izo*, ndi *zinazo*.” Izo

sizinaululidwebe, mwaona, ayi, nkomwe. O, m'bale, tangoonani kumene . . .

Ife tiyenera kuti titseke, chifukwa ndi thwelofu koloko.

175 Zindikirani, kuyesetsa kuti akutchingeni inu kuti musawone tanthauzo la Mawu a m'badwo uno, la Kuwala kwamadzulo kukutanthauziridwa. Izo ziri . . . Kodi izo zikutanthauza chiyani? Ndi nthawi ya kutuluka imene ili pafupi, Mulungu akudzera Iye, motsimikiza basi monga dziko. Mukuona?

176 Tsopano ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu funso. Pamene, ndi thwelofu koloko tsopano, adutsa maminiti faifi; ndipo ife tipitiriza, usikuuno. Kodi inu mukumuwona mulungu wa m'badwo uno? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira izo? ["Ameni."] Mukuona momwe izo ziliri, mpingo, waluntha, sayansi?

Dziko lonse ndi lake, mwaona, zipembedzo. Ndipo, inu mukuti, "Ndine Mkhristu." "Kodi ndi chipembedzo chiti chimene inu mulimo?" Chabwino, ngati ine nditakhala wa chipembedzo, ine sindikukhulupirira kuti ine ndingakhale Mkhristu. Tsopano, amenewo ndi mawu aakulu, koma izo nzoona.

Ine ndamaliza kumene kunena kuti chidziwitso ndi sayansi, ndi Chikhristu, ziribe nkomwe ubale uliwonse. China ndi cha mdierekezi, ndipo chinacho ndi cha Mulungu. Chirichonse chimene chimakana Mawu a Mulungu, mutalikirane nacho icho. Mukuona? Ayi, bwana. Baibulo likuitanira, masiku otsiriza ano, kuti Akhristu atulukeko kwa wachiwerewere ameneyo, umenewo ndi mtengo wa chabwino ndi choipa.

177 Ndithudi, iye ali nazo zabwino. Kodi aliyense angalankhule choipa cha chipatala? Ayi, bwana. Laibulale? Ayi, bwana. Maphunziro? Ayi, bwana. Koma, mwaona, iwo akuwapatsa iwo zimenezo wopanda Mawu. Mukuona momwe izo ziliri zonyenga? Kuwapatsa iwo tchalitchi choti azipitako, kupembedza koti azipembedzako, "mulungu atakhala pa mpandowachifumu." Baibulo linaneneratu izo.

178 Tsopano ndinu wa lirilonse la magulu amenewo. Alipo awiri okha a iwo pa dziko lapansi lero, nthawizonse zakhala zili, ndipo zidzakhalapo kufikira Yesu adzabwere, ndipo limodzi la ilo lidzawonongedwa. Tsopano ndinu wa limodzi la magulu amenewo. Limodzi la ilo, inu mumajowina; linalo, inu mumabadwira mwa Ilo. Mukuona?

Limodzi la ilo, ndinu gawo lake chifukwa inu munabadwira mwa Ilo. Inu muyenera kukhala gawo la Ilo. Kodi ine ndingakane kuti ndiri ndi dzanja? Chimodzimodzinso kuti ine sindingakane Mawu aliwonse a Mulungu, ngati ndine gawo la Mulungu. Ndine gawo la William Branham; ine ndiri mzigawo, ndipo gawo lirilonse ndi gawo la ine. Ndipo Mawu aliwonse a Mulungu

ayenera kugwirizana ndi mzimu wanga, liyenera kukwanirana ndi moyo wanga, liyenera kukwanirana ndi makhalidwe anga, liyenera kukwanirana ndi malingaliro anga. Ngati malingaliro anga ndi osiyana ndi Iwo, ndiye kuti Mzimu wa Mulungu sukukhala mwa ine. Izo nzoona. Sindingakane Mawu amodzi a Iwo.

179 Inu muli wa limodzi la maguluwo. Muyenera kutero, izo ziyenera kutero basi. Mwina ndi Thupi la Mulungu, limene liri mwa Mawu; kapena thupi la Satana, mwa mpingo. Ndipo dziko lonse liyenera kukhala la mpingo winawake; ilo limapembedza mulungu winawake. Iwe uyenera kuti umapembedza mulungu wa chidziwitso, iwe umadalira pa zomwe iwe umamva mwa chidziwitso, iwe umadalira pa *izi*, kapena *izo*, kapena *zinazo*; kapena iwe umadalira Mawu a Mulungu, mwa chikhulupiriro, kumuyembekezera Iye kuti awatsimikizire Iwo ndi kuwapanga Iwo kukhala owona.

> Mpingo weniweni wa Mulungu ukuyembekezera kudza kwa tsiku lokondwa la Zakachikwi,
> Pamene Ambuye wathu wodala adzabwera ndi kudzatenga Mkwatibwi Wake woyembekezera;
> O, mtima wanga wadzadza ndi mkwatulo pamene ndikuvutikira, kupenyerera ndi kupemphera,
> Pakuti Ambuye wathu akubwereranso ku dziko.
>
> O, Ambuye wathu akubwereranso ku dziko,
> Satana adzamangidwa zaka chikwi, sitidzakhalanso ndi wotiyesa,
> Yesu akadzabweranso ku dziko.

180 O, anthu a United States uyu, kumene Uthenga uwu ukupita tsopano, thawani zolimba mmene inu mungathere ku chidziwitso ichi, m'badwo wa sayansi umene ife tiri nkukhalamo. Thawirani ku Mawu a Mulungu!

Inu, ine, palibe amene angathe—angathe, kuwadziwa Iwo. Palibe amene angawatsimikizire Iwo. Mulungu amachita kutsimikizira Kwake Kwake. Palibe aliyense yemwe ali nawo ufulu wotanthauzira Iwo; ine, palibe munthu aliyense yemwe ali nawo ufulu. Mulungu amachita kutanthauzira Kwake Kwake. Iye anapanga lonjezo. Iye anati akanadzachita izi mmasiku otsiriza.

Ndipo mmasiku otsiriza mulungu wa m'badwo woipa uno adzachititsa khungu maso a anthu, ndi luntha lake lachidziwitso, pa mtengo wosakanizikirana wa chabwino ndi choipa, kumawapatsabe iwo anthu. Ndipo apa pakubwera, chinthu chija chikukwera mmwamba, chipembedzo chija

kuchokera kumbuyo uko mu Mibadwo ya Mdima, ndinso Mibadwo ya Mdima isanafike, zonsezo zikukwera kufika kwa mwamuna wapamwamba, Satana, amene anati, "ine ndidzazikweza ndekha pamwamba pa ana a Mulungu, ndipo iwo adzandimvera ine." "Ndipo iye monga Mulungu azidzakhala mu kachisi wa Mulungu, ndipo ana a Mulungu adzagwera zimenezo."

181 Bwanji, mwana wa Mulungu, akuti, "Chabwino, mkazi wanga, izo siziri; iye ndi wabwino . . . " Pitirirani, kazipitiririrani. Mukuona?

Inu mukuti, "Chabwino, Iye anati 'ana aamuna a Mulungu.'" Inde, bwana.

Mwamuna, aliyense yemwe iye ali, anapangidwa mu chifanizo cha Mulungu, kwa ulemelero wa Mulungu. Ndipo mkazi ndi chotuluka mwa mwamuna, osati kwa Mulungu. Kulondola. "Pamene ana a amuna a Mulungu anawawona ana aakazi a anthu kuti anali okongola, iwo anadzitengera kwa iwo akazi."

"Ndipo monga izo zinali mmasiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu."

Tsopano taonani, ngati inu mukufuna kudziwa malo amene mpingo uli, muwone malo amene akazi ali, mwaona, chifukwa iyeyo ndi mpingo. Muwone zimene iye akuchita, mwaona, ndipo mu m'badwo uno wa wachiwerewere.

182 Taonani, kunalibeko mzinda woyipitsitsa, woipa, wotsikitsitsa, wachiwerewere mu dziko, kuposa Nazareti, ndipo kuchokera mmenemo Mulungu anasankha namwali. "Kodi chinthu chabwino chirichonse chingatuluke kuchokera mu Nazareti?"

Ndipo kuchokera mu m'badwo woipa uno, mmene mulungu wa m'badwo uno wawachititsa khungu maso a anthu, ndi miyambo yawo ndi zipembedzo; kuchokera mu m'badwo uwo kumene, Mulungu akusankha anthu kwa Dzina Lake.

Ngakhale kuno okanidwa ndi onyozedwa,
tsiku limodzi Ambuye adzabweretsa
Osankhidwa Ake mkati mwa chipata, ndipo
ndi zoyenera chirichonse kwa ine.
Ndiye tidzaimba ndi kufuula, ndipo tidzavina,
Mwanawankhosa adzapukuta misonzi yathu;
Tidzakhala nalo sabata limodzi lobwera
kwathu,
Zaka chikwi khumi zoyambirira. (Uko
nkulondola.)

Anthu odabwitsa kwa Dzina Lake ndipo akutchedwa Mkwatibwi Wake. (Nkulondola uko?)
Ngakhale kuno okanidwa ndi onyozedwa, tsiku limodzi Ambuye adzabweretsa
Osankhidwa mkati mwa chipata, (mu kutuluka) ndipo ndi zoyenera chirichonse kwa ine.

183 Ine ndikuyamba kukhala bambo wokalamba. Ndipo masiku anga akuyamba kuzilala; ndipo kupenya kwanga kukuyamba kuthima; ndipo lawi langa laling'ono la moyo likuyamba kuyaka mozirala. Ine sindikuwopa mdima. Chifukwa ine ndikufuna kuti ndinene izi, ndi Paulo, "Ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiukitsiro Chake." Ziribe kanthu kuti iwo adzandikwirira ine kuti, ngati ine ndidzamira mnyanja, kapena kudzawotchedwa mu ng'anjo, kapena kudyedwa ndi mkango, Iye adzaitana dzina langa, ndipo ndidzalankhula. Ameni!

Tiyeni tipemphere.

184 Ngati alipo muno, kapena kunja pa mawaya a Uthenga uwu kudutsa fukoli, mu matchalitchi anu aang'ono ndi magulu ndi maholo, kulikonse kumene inu mwakhala, ngati alipo mmodzi, o, mundilole ine ndikuchondelereni inu; mundilole ndikupempheni inu, ngati mtumiki wa Uthenga; mundilole ndikupempheni inu, mu Dzina la Yesu Khristu; thawani mkwiyo wa m'badwo woipa uno! Musamatumikire mulungu wa m'badwo woipa uno.

O, ine ndikudziwa inu mukuti, "Ndi zabwino. Iwo ndi abwino." Ndendende, mtengo wosakanizikana. Inu simungathe kusakaniza chidziwitso ndi Mawu a Mulungu.

Iwo ndi Mawu amene ayenera kukhulupiriridwa mwa chikhulupiriro, osati chidziwitso. Inu simumamvetsa Iwo; inu mumawavomereza Iwo. Inu mumati Iwo ndi owona, ndiyeno inu mumakhala moyo Wake. Ndizo zonse zimene Iye akukufunsani inu kuti muchite.

Ngati alipo aliwonse muno mu gulu lathu, ife sitingathe kuitanira paguwa kuti tikubweretseni inu kuno, chifukwa kulibeko malo aliwonse; kapena uko pa wailesi, pa zingwe za lamya, ngati alipo aliwonse kumeneko amene sakumudziwa Iye. Musati . . .

185 O, akazi, ine ndakuzazirani inu mmawa uno, osati ine, ine ndimangobwereza mowerenga Mawu. Tsitsi lalifupi, kumavala zovala zazing'ono zakale izo, kumadziveka nokha mmawonekedwe enieni oyambitsa chikhumbo chogonana, kodi inu simukuzindikira kuti mzimu umene. . .Inu mukhoza kukhala woyera, mlongo, wokondedwa, pamene izo zifika kwa thupi lanu, koma mmoyo mwanu kodi inu simukuwona chimene chakugwirani inu?

Kodi Mulungu angamupange mwana Wake wamkazi kuti aziwoneka wachikhumbo choyambitsa kugonana kuti akanyenge mwana Wake yemwe wamwamuna, kuti azikamusilira iye, kuti akawapange onsewo kukayankhira chigololo? Kodi Iye angachite zimenezo, mlongo? Mudzifunse nokha funso limenelo. Ayi, osati mwa mamailosi teni milioni. Musaziike zimenezo kwa Mulungu.

186 M'bale, kodi mulungu wakupatsani inu mzimu wa dziko lino mpaka inu mukulephera kuwona kuti izo ndi zolakwika? Kodi iye wachititsa khungu maso anu, ku mbalume za mpingo, chipembedzo, kachikhulupiriro, ndi zina zotero, mwakuti inu mukulephera kuwona kuti Mulungu akuwatsimikizira Mawu Ake ndipo akuwapanga Iwo chomwecho? Kodi ntchito yanu, abwana anu, mkazi wanu, ana anu, mpingo wanu, kapena chirichonse, chakulekanitsani inu ku Mawu a Mulungu, amene ali gwero lokhalo la Moyo? Muthawe zimenezo, m'bale wanga! Ine ndimakukondani inu, ndi chikondi chaumulungu. Ine sindimalemekeza aliyense wa abale anga kuposa inu, ayi nkomwe. Ngati ine nditatero, ine ndingasonyezere kulemekeza kwa munthu. Ine sindikunena zinthu izi kuti ndikukwiyitseni inu. Ine ndikusonyeza, ndikunena zinthu izi chifukwa izo ziri mu Mawu a Mulungu. Ndipo ngati wantchito wa Mulungu, ndi chikondi cha Mulungu mu mtima mwanga, ine ndikukuuzani inu zinthu zimenezo kuti inu mukawone ndi kuzimvetsa. Mwinamwake inu simukanadziwa ngati ine ndikanapanda kukuuzani inu. Kodi inu muthawa izo lero?

Tsopano, ndi kulikonse kudutsa dzikoli, tiyeni tiweramitse mitu yathu.

187 Wokondedwa Mulungu, patsogolo panga pali mipango. Anthu akudwala; ine ndikuika manja anga pa iyo, kuti Inu muwachize iwo.

188 Ndipo ine ndikudalira, Ambuye, usikuuno, kuti kukhala msonkhano wawukulu, kuti Mphamvu ya Mulungu ikhala pano, zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa. Monga ife tamvera zotsatira kuchokera mmisonkhano ingapo yotsiriza iyi, ndi zopambana bwanji, kuwona zimene zachitika! Ine ndikupemphera, wokondedwa Mulungu, kuti Inu mutipatse ife magawo awiri usikuuno. Ine ndikupemphera izo ndi mtima wodzipereka, Ambuye, chifukwa ndi chikondi changa kwa Inu ndi Mawu Anu, ndi kwa anthu awa. Perekani izi, wokondedwa Mulungu.

189 Ndipo ngati uko kudutsa dzikoli, kapena ngakhale kuno tsopano, kuti kuli ena amene akudwala ndi osautsika, ndipo ayenera kukhala atapita usikuuno, sakhala pano, kapena akukhala kunja uko mmatchalitchi kapena malo kumene iwo amakomanako; ine ndikupemphera kuti Inu mukawachizeko iwo. Tsopano, Ambuye, koma kwa machiritso onse aakulu

kwambiri! Ngati inu muti muchiritse thupi lawo ku khansa, TB, chibayo, chinachake, iwo adzadwalanso, sindikukaikira, ngati iwo ati akhale moyo nthawi yaitali, pakuti thupi lawo likadali panobe pansi pa tchimo, themberero. Koma muwalole iwo alandire—machiritso Auzimu enieni, kuchiritsidwa kwa moyo wawo, zimene zimapanga cholengedwa chatsopano, kudutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo, ndiyeno nkumadikirira mu msasa wakale uwu chiwombolo cha thupi moyowo utatha kuwomboledwa. Perekani izi, Ambuye.

190 Mulole iwo athawe zipembedzo zimenezo ndi tizikhulupiriro. Mulungu, kutali uko mu tizikhulupiriro timeneto ndi zipembedzo ine ndakumanapo nawo ena a abale abwino kwambiri. Ndipo, Mulungu, ine ndinganene bwanji kuti iwo awone, ndi kuwalola iwo kuti awawone Mawu? Izo zimandisautsa ine. Koma ine ndikudziwa, panonso, kuti Inu munati, "Palibe munthu amene angadze," ziribe kanthu kaya ndi wabwino bwanji, wofatsa bwanji, wodekha bwanji, "pokhapokhapo Atate Anga atamuitana iye. Ndipo onse amene Atate Anga andipatsa Ine, iwo adzadza." Ndipo, Ambuye, ine ndikumverera udindo wanga wokhawo ndi wonena Choonadi.

Ndipo osati monga Paulo anati, "Kuwagwira Mawu a Mulungu ndi chinyengo," ndi mwambo wa chipembedzo utasakanizika mwa Iwo, monga mtengo wosakanizika wa chabwino ndi chidziwitso, chabwino ndi choipa; koma ndi mtima wotseguka ndi Mzimu Woyera. Perekani izi, Mulungu. Mumupulumutse wina aliyense.

191 Tsopano ndi mitu yathu yoweramitsidwa ndi maso athu atatsekedwa. Ndipo osati kwa ine. . . ine sindinganene izi mwanjira iyi, "Izo sizindisintha ine kaya inu mukachita kapena ayi." Izo zimandisintha ine. Ine ndimakukondani inu. Ndipo ine ndikuyembekeza inu simukuganiza kuti ndi chifukwa chake ine ndiyenera kulankhula mwaukali . . . Monga ananenera Paulo, "Ine ndikukhumba ndikadakhala limodzi nanu, ndipo ine ndikadasintha kachitidwe kanga." Izo sizinali chifukwa chakuti iye samawakonda iwo; iye ankawakonda iwo. Ayi . . . Monga Yesu anachita kuwadzazira iwo, ndipo kenako nkuwafera iwo. Mwaona, "Atate, akhululukireni iwo; iwo sakudziwa nkomwe zimene iwo akuchita." Taganizani, munthu amene akufuna kuti achite bwino, ndipo akuyesetsa kukhala molondola, ndipo nkumuwona mdierekezi ameneyo . . . Ndiye yekhayo amene ine ndikutsutsana naye, amene wachititsa khungu maso a anthu awa.

192 Fuko lino liyenera kumayaka ndi ulemelero wa Mulungu, powona zimene zachitika mwa ilo mu tsiku lotsiriza lino, lotsiriza ili. Nchifukwa chiyani zitsitsimutso izi sizinagunde maiko akale? Ili ndi Gombe la Kumadzulo kuno, kumadzulo kutali kwambiri kumene iwe ungathe kupita. Tsopano chotchinga cha tchimo chabangula pansi pa dziko lapansi, ndipo

ilo likumira; malo, ndipo Los Angeles ndi Hollywood, akumira mainchesi ambiri pa ora, palibe njira yoti angaziletsere izo. Eya, ife tiri pano. Pafupifupi nthawi iliyonse ife timva kuitanako. Ngati inu mukudziwa zimenezo . . .

Tsopano, aliyense asayang'ane. Koma ngati inu mukudziwa, kuchokera mu mtima mwanu . . . Ine ndikukufunsani inu. Ine sindingathe kuwudziwa mtima wanu, pokhapokhapo Mulungu atawulula izo. Koma kuchokera mu mtima mwanu, ngati inu mukuona kuti inu simuli pamene inu mukuyenera kukhala ndi Mulungu ndi Mawu Ake, mwa chikhulupiriro, kodi inu mungangokwezera kwa Iye dzanja lanu, kunena kwa Iye, "Ambuye, mundithandize Inu ine." O Mulungu! Kuchokera pa mpingo pano, padzadza, padzadza kuzungulira makoma, mkati ndi kunja, kwenikweni mazana a manja, mwinamwake manja mazana awiri akwezedwa mmwamba. Zikomo inu chifukwa cha kuwonamtima kwanu.

193 Wokondedwa Yesu, musalole mmodzi wa iwo ataike. Ngati wantchito Wanu, amene amaima pakati pa amoyo ndi akufa, ndikuwalozera iwo, ndi chala, ku Mawu a Mulungu. Ine sindingathe kuwapulumutsa iwo, Ambuye, koma iwo akufuna kuti apulumutsidwe. Ndipo, Ambuye, monga ine ndanenera nthawi zambiri, dzuwa limatulukira kummawa; ndipo pamene ilo likukwera kudutsa pa dziko lapansi, ilo limatumizidwa ndi Mulungu kuti likachetse njere, kuti likapange chakudya chathupi kwa moyo wathupi. Koma, O Mulungu, Inu munati, "Kwa iwo amene awopa Dzina Lake Dzuwa lachirungamo lidzawawalira ndi machiritso mmapiko Ake." Mulole Dzuwa lachirungamo, Mawu a Mulungu, litulukire mmitima ya anthu, ndi milozo ya chikhulupiriro cha machiritso mu Mawu amenewo ichiritse wosamvera aliyense ku Mawu, ndi kuwabweretsa iwo kufikira chidzalo cha ana aamuna ndi ana aakazi a Mulungu.

Iwo ndi Anu, Ambuye. Mu Dzina la Yesu Khristu, konse kuwiri kuno ndi kunja uko pa wailesi, ine ndikuwapereka iwo amene anakweza manja awo kwa Inu kwa chipulumutso cha miyoyo yawo. Ameni.

Uko moyo wanga wokwatulidwa udzapeze
(Kuti? Pa guwa ili.)
Mpumulo kutsidya . . . (mwa chikhulupiriro ine
ndikuyang'ana uko kumene ine ndikupita)

Pafupi ndi mtanda, (ndiko kumene Mawu
apachikidwako) . . . mtanda,
Ndidzitamandire;
Moyo wanga ukwatulidwire
Mpumulo kutsidya la mtsinje.

Yesu, mundisungetu . . . (Ndiko, kupachikidwa
ndi Iye, sindikufuna kalikonse ka mdziko.
"Mundisunge ine wopachikidwa.")

Kuli kasupe wokoma,
Ndi waulere kwa onse, mtsinje wochiza,
Wosefukira kuchokera ku Kalvare.

Mu mtanda, mu mtanda,
Ndidzitamandire (tiyeni tikweze manja athu) nthawizonse;
Moyo wanga ukwatulidwire
Mpumulo kutsidya la mtsinje.

194 [M'bale Branham akulankhula tsopano kwa a zing'wenyeng'wenye—Mkonzi.] "Ine ndikutha kumumva Mpulumutsi wanga akuitana."

Fikirani ndipo mugwire dzanja la winawake, ndikuti, "Mulungu akudalitseni inu, Mkhristu."

[M'bale Branham akulankhula kachiwiri ndi azing'wenyeng'wenye—Mkonzi.] "Ine ndikutha kumumva Mpulumutsi wanga akuitana."

Kodi inu mukumverera Kukhalapo Kwake? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.]

Kunja uko pa mipweya ya lamya, inu nonse mugwirane chanza wina ndi mzake kumeneko, ndikuti, "Mulungu akudalitseni inu, Mkhristu."

195 Inu mukudziwa, kuli dziwe la madzi kumbuyo kuno. Iye akutenga anthu amene avala Dzina Lake. Inu simunabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu, tiri ndi dziwe, tiri ndi zovala, kuli munthu yemwe waima atakonzeka. Inu muli olandiridwa, ngati inu mukumuvomereza moona Yesu ngati Mpulumutsi wanu ndipo mukukhulupirira kuti izo ndi Choonadi.

196 Kumbukirani, simunayambe mwakhalapo munthu mu Baibulo, kapena nthawi iliyonse usanachite bungwe mpingo wa Katolika, anayamba wabatizidwapo mwanjira ina iliyonse yosiyana ndi mu Dzina la Yesu Khristu. Mulibemo malo opezeka mu Lemba, kapena mbiriyakale, kuti anthu aliwonse anayamba abatizidwapo, mu Mpingo wa Mulungu wamoyo, mu dzina la maudindo a "Atate, Mwana, Mzimu Woyera." Iwo ndi mwambo wa Katolika, ndipo osati kuphunzitsa kwa Baibulo.

197 Ndikufunsidwa ndi wansembe, ine ndinamufunsa iye zimenezo. Iye anati, "Izo ndi choonadi. Koma ife ndi mpingo; ife tikhoza kusintha chirichonse chimene ife tikufuna. Ulamuliro uli mu mpingo. Mulungu ali mu mpingo Wake."

198 Ine ndinati, "Mulungu ali mu Mawu Ake. Ndipo ngati mpingo uli..." Ine ndinati, "Mulungu ali Mawu. Ndipo ngati mpingo ukutsutsana ndi Mawu, ndiye ine sindingawukhulupirire mpingowo."

Ine ndimasiya mawu a munthu aliyense akhale bodza, kaya ndi wansembe, papa, chirichonse chimene chingakhale, ndipo Mawu a Mulungu akhale owona.

Ndipo Paulo anapangitsa munthu aliyense, ziribe kanthu kuti iye anabatizidwa chotani, ngati iye sanabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, kuti abwere ndi adzabatizidwenso kachiwiri.

199 Ndipo ena atatha kale kulandira Mzimu Woyera, Petro anati, "Kodi ife tingaletse madzi, powona kuti awa alandira Mzimu Woyera," Machitidwe 10:49, "powona kuti awa alandira Mzimu Woyera monga ife tinachitira ku . . . " Ndipo iye anawalamulira iwo, "Musanachoke pa malopo, ngakhale inu mwalandira Mzimu Woyera, mubwere ndipo mudzabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu."

Pakuti, Petro anapatsidwa fungulo ku Ufumu, anati, "Chirichonse chimene inu mudzamanga pa dziko lapansi, Ine ndidzachimanga icho Kumwamba." Ndipo kodi fungulo limachita chiyani? Ilo limatsegula chinachake, chinsinsi.

200 Ndipo pamene Yesu anati, "Pitani, mukawabatize iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera," anaika zimenezo apo kuti zikamchititse khungu wosakhulupirira.

Penyani! Nchifukwa chiyani Petro sanakachite zimenezo, mawu pa mawu? Iye ankayenera kutero.

Ngati munthu abatizidwa mu maudindo, "Atate, Mwana, Mzimu Woyera," iye sanabatizidwe nkomwe; iye alibe Dzina. *Atate* si dzina, *Mwana* si dzina, ndipo *Mzimu Woyera* si dzina. Mzimu Woyera ndi chimene Iwo uli; monga, ine ndine munthu. Iwo ndi Mzimu Woyera.

*Atate* ndi udindo; ndine atate. *Mwana* ndi udindo; ndine mwana. *Munthu* ndi udindo; ndicho chimene ine ndiri. Koma dzina langa ndi William Branham.

Ndipo Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera ndi Dzina la "Yesu Khristu." Yesu anati, "Ine ndinadza mu Dzina la Atate Anga." Kodi Dzina la Atate ndi liti? Mwana aliyense amabwera mu dzina la atate ake. Ndipo Dzina la Atate ndi Yesu Khristu. Mukuona? Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

201 Ngati ine nditakuuzani inu kuti mupite uko ndipo mukanditengere ine chinachake kuchokera pa alumali kumusi kuno, mu dzina la ameya a mu mzinda. Ndi angati akuwadziwa ameya a mu mzinda? Mzanga wabwino, Rich Vissing. Chabwino, inu simungapite kumusi uko ndi kukati "mu dzina la a meya a mzinda." Inu mukati, "Mu dzina la Richard Vissing." Anthu inu kuno mu Jeffersonville mukudziwa yemwe iwo ali.

Ndipo ndicho chifukwa Iye anati, "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Mwa Iye mukukhala Umulungu, chidzalo cha Umulungu mthupi. Iye anati, "Mukawabatize iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera."

202 Petro ataima pamenepo ali ndi vumbulutso pa chimene Iye anamangirapo Mpingo, a Yemwe Iye anali, iye anati, "Mulape, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu." Ndipo palibe . . . Mafungulo anatembenukira Kumwamba ndi pa dziko lapansi. "Kulibeko Dzina lina pansi pa Kumwamba linapatsidwa pakati pa anthu limene inu muyenera kupulumutsidwa nalo."

203 Nchifukwa chiyani inu mumabatiza mu Dzina la Yesu Khristu? Kwa chikhululukiro cha machimo. "Machimo a aliyense amene inu mudzawakhululukira, kwa iwo akhululukidwa." Mukuona? Koma ngati inu simukuwona kuti ndi woyenera ndi wokwanira kuti abatizidwe, inu musachite zimenezo. Pakuti, pamene inu muchita izo, izo zimachita zimenezo, mwaona. Kodi inu mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza?

> Ndikukhoza kumva Mpul- . . . (Mawu) akuitana, (akuitana kumusi uko kumanda)
> Ndikukhoza . . . ("Kodi inu simufa limodzi ndi Ine, kuti inu mudzathe kuwuka ndi Ine?") . . . -umutsi akuitana,
> Ndikukhoza kumva Mpulumutsi akuitana, (kodi dziko linena chiyani?)
> "Tenga mtanda, ndipo unditsate, unditsate . . . "

Tsopano, ngati inu simunatero:

> Komwe Iye (Iye ali Mawu) anditsogolera ine . . . (tiri ndi dziwe)
> Komwe Iye anditsogolera ine ndidzamtsatira,
> Komwe Iye anditsogolera ine ndidzamtsatira,
> Ndinka Naye, Naye njira yonse.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

204 Wokondedwa Mulungu, dziwe lakonzeka. Tsopano mulankhule ndi mitima, Ambuye. Mulole iwo amumve Khristu, Mawu, akuwaitana iwo, ndipo apite naye Iye njira yonse.

"Ine ndinka Naye kudutsa mmundamo. Ine ndipita Naye waku dziwe. Ine ndidzatenga Dzina Lake. Ine ndikufuna kuti ndikhale mmodzi wa anthu amene Iye akuwaitana kwa Dzina Lake. Ine ndikhulupirira Mawu Ake. Ine ndidzamtsatira. Ine sindidzadzivula ndi dziko. Ine ndidzakhala Mkwatibwi woona, wotomeredwa. Ine sindidzasiya mtsempha umodzi wa Mawu Ake. Chopempha chirichonse, ine ndidzakhala weniweni, Mkwatibwi woona. Chirichonse chimene Iye andipempha ine kuti ndichite, chimenecho ine ndidzachichita.

"Ngati Mwamuna wanga amene akubwera akufuna kuti ine ndilisiye tsitsi langa lizikula, ine ndichita zimenezo. Ngati Iye akufuna kuti ine ndichotse zozipakapaka zonse izi, ine

ndichita izo. Ngati Iye akufuna...Iye akandiuza ine kuti ndi mzimu woipa, woipa umene ine ndikuvula nawo, ndi zovala zowoneka mwachigololo izi; ine ndidzachita zimenezo, ine ndidzazivula izo. Ine sindisamala zimene wina aliyense anganene, ine ndidzazivula izo.

"Iye akafuna kuti ine ndichoke mu gulu ilo limene ine ndiri nalo, la osakhulupirira, ine ndidzachita zimenezo; ngakhale ine nditapanga mkate wanga, kapena chirichonse chimene chiri. Iye analonjeza Iye sadzandisiya ine ngakhale kunditaya ine. Ine ndidza—ine ndidzachita zimenezo. Ine ndidzapita naye Iye njira yonseyo. Iye akafuna kuti ine ndibatizidwe mu Dzina Lake, ine ndidzachita zimenezo."

Ambuye, Inu munalonjeza izo mu Mawu Anu apa, ndizo zimene Inu mumafuna. Mulole munthu aliyense awone izo, Ambuye, ndipo mokoma, modzichepetsa awerame kwa Ilo. Mu Dzina la Yesu ine ndikupemphera. Ameni.

205 Inu muli a Mulungu. Mulole Mulungu atenge mawu pang'ono oswekawa ndipo awapange iwo akhale enieni kwa inu, ndiro pemphero langa loona.

Dziwe likhala lokonzeka. Aliyense amene akufuna kuti abwere, iwo ali...Mtumiki alengeza zimenezo kanthawi kena. Aliyense amene walapa ndipo akufuna kuti abatizidwe, pogwiritsa ntchito Dzina la Yesu Khristu, inu mungobwereratu. Chirichonse chakonzeka. "Zinthu zonse zakonzeka." Chirichonse chimene ife tingathe kuchita kuti tikuthandizeni inu kuti muzikhalira moyo Mulungu, ife tiri pano kuti tichite zimenezo. Mulungu akudalitseni inu.

206 Tsopano tiyeni ife tiimirire. Tsopano nyimbo yathu yaing'ono, *Ine Ndinkonda Iye*. "Ine ndinkonda Iye chifukwa Iye anayamba kundikonda ine." Tiyeni tiimbe iyo, aliyense tsopano.

> Ine ndinkonda Iye,. . .

Tiyeni tikweze manja athu pamene ife tikuimba iyo.

> . . .ndinkonda Iye
> Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
> Nandigulira chipulumutso changa
> Pa mtengo wa Kalvare.

Ndi mitu yathu yoweramitsidwa ndi mitima, tiyeni tiing'ung'uze iyo kwa Iye. [M'bale Branham akuyamba kung'ung'uza *Ine Ndinkonda Iye*—Mkonzi.]

> Ine ndinkonda Iye.

[M'bale Branham akupitiriza kung'ung'uza *Ine Ndinkonda Iye*—Mkonzi.]

O Mulungu, Atate wathu, tichitireni chifundo ife zolengedwa zosauka, Ambuye. Tilimbikitseni ife chifukwa cha ntchito

imene ili patsogolo pathu. Mundithandize ine, O Mulungu, mundithandize ine! Ine ndikumverera kuti chinachake chiri pomwe pano, Atate. Mundithandize ine, O Mulungu, kuti ndidziwe Choonadi. Adalitseni anthu awa, wokondedwa Mulungu. Atsogolereni iwo, ine ndikupemphera, mu Dzina la Yesu.

207 Tsopano pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, ine ndiwapempha abusa pano, M'bale Neville, m'bale wathu wofunika, abwere pano tsopano ndipo adzanene zimene iye atanene, zokhudza…zokhudza ubatizo. Ine ndikhoza kulengeza zimenezo. Ine ndikuganiza dziwe latsegulidwa, kale.

*Mulungu Wa M'badwo Woipa Uno* CHA65-0801M
(The God Of This Evil Age)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingelezi Lamlungu mmawa, Ogasiti 1, 1965, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2018 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org